BUKHU

[LOMASULIRIDWA]

LA

CHIVUMBULUTSO

BUKHU 2
[CHAPUTALA 4-8]

Kwa
Mkwatibwi wa Khristu
Bukhu ili laperekedwa

BUKHU {LOMASULIRIDWA} LA CHIVUMBULUTSO

Ben Howard

Translated To Chichewa Language
By
Enoch Kamanula
New Testament Assembly
P.O. Box 64
Mwanza-Malawi

KUSINDIKIZIDWA KOYAMBA 1980

KUSINDIKIZIDWA KACHIWIRI 2005

Palibe gawo la bukhu ili limene lingachulukitsidwe [kupatula lemba la Baibulo] popanda chilolezo cholembedwa. Kuti mumve zambiri lemberani ku:

Sound of Liberty
Ben Howard
7286 Hwy 53W
Dawsonville, Georgia 30534 (USA)
TwoAnds@soundofliberty.org
www.SoundofLiberty.org

MALONJE

Bukhu la Chivumbulutso ndi bukhu la zoimirira, limene; politanthauzira, ndi uneneri wapamwamba. Ili si bukhu limene likuchita ndi chiphunzitso kapena ziphunzitso za maziko zimene zinabwera kwa ife ndi mtumwi Paulo ndi alembi ena a malemba za m'mene tingapulumutsidwire kapena m'mene tingalandirire dongosolo la chipulumutso la Mulungu.

Bukhu la Chivumbulutso linalembedwa mu 96 A.D. mpingo utagwa ku chikondi chake choyamba. [Chivumbulutso 2:4] Chikuonetsa m'mene mpingo unathera kudutsa mu nthawi mu maonekedwe ake akugwa. Chikuonetsanso [ndipo mofunika kwambiri] mpingo ukubwezeretsedwa ku malo ake a pachiyambi kuno ku nthawi yotsiriza.

Mpingo wapachiyambi sunagwe kuchokera ku bukhu la Chivumbulutso, chifukwa sunali gawo la malangizo wolembedwa kwa mpingo kuchiyambi. Ndi bukhu la mwala wapangodya, ndipo osati bukhu la maziko, ndipo kotero ndilongomasuliridwa kwa mpingo pano pa nthawi yotsiriza. Ndi kalata wa chikondi wa Mulungu kwa mkwatibwi, ndipo Khristu akupanga chikondi ndi mkwatibwi wake pamene Iye akumupatsa iye mzimu wa vumbulutso ndi kuulura zinsinsi kwa iye. Ichi ndi chifukwa cha bukhuli, **"Bukhu [lomasuliridwa] la Chivumbulutso."** Ndi Mulungu kuika Chisomo Chachikulu [Machitidwe 4:33] pa mpingo wake mkwatulo usanachitike.

Komanso, mundirole ndilankhule, kuti owerenga ambiri a bukhu la Chivumbulutso alakwitsa potenga Yohane, mlembi, ngati Yohane nkonzi wa bukhu. Koma palibe njira iliyonse tinganene molondora kuti Yohane ndi nkonzi wa bukhu la Chivumbulutso. Iye anali mlembi, chotengera chabe chimene Mulungu anagwiritsa ntchito kufalitsa malingaliro Ake ku Mau olembedwa kuti awuluridwe pano mu nthawi yotsiriza. Yesu anali, ndipo ndi nkonzi wa bukhu la Chivumbulutso.

Momwemonso olemba bukhu ili akuzindikira mochuluka kuti NKONZI wa bukhu la Chivumbulutso ndi amene wapereka kudzoza kwa kumasulira kwenikweni kwa mlembi uyu. Kotero, ine ndikupemphera kuti mwapemphero inu mutenga kumasulira kwa bukhu la Chivumbulutso chifukwa Mkwatibwi wa Khristu adzamvetsa bwinobwino zimene zikuchitika pano mu nthawi yotsiriza, chifukwa kuwala kwake [kumvetsa] ndi kowala ngati krustalo. [Chivumbulutso 21:11]

Komanso, ndiloreni ndinene ine -Ben Howard- kuti: kwa zaka zoposa 45 ndakhala ndikutumikira pa zolembedwa zimene zili mu bukhu ili, ngati mishonare mu maiko ambiri ndi kuno ku USA, mu mipingo, maholo, madera, nyumba zobwereketsa, ngati mlaliki wa pa wailesi, kufunsidwa mafunso, ndipo tsopano pa Internet, ngati m'busa wa **Sound of Liberty Assembly** moyandikana ndi Dawsonville, Georgia [USA] ndi mitundu ina ya malo wopezekamo anthu. Mwambiri mwa malo olankhulawa, kufunsidwa mafunso ndi zina, panali kujambulidwa matepi komanso kutenga mfundo zolemba pa zimene zimalankhulidwa zimene ine tsopano sindingathenso kuzilamulira.

- Kotero, zidziwike kwa onse: Kuti bukhu ili lapambana, ndipo laposa, zolembedwa zonse, zojambulidwa kapena mitundu ya nkhani zonse zotengedwa kuchokera kwa mlembi zimene zikuoneka ngati- kapena- zikutsutsana ndi zolembedwa izi, ngati zimenezo zinatengedwa mbuyomu lisanasindikizidwe bukhuli.
- Ichi ine ndikunena, chifukwa maulaliki ambiri pa matepi, ma CD, ma DVD, ma Video, komanso pa Internet apita ku madera ambiri padziko lonse kwa zaka zambiri zimene muli

zochepa, ndipo mauthenga ena akale akhoza ngakhale kutsutsa zolemba izi, ine ndachita monga 2 Petro 3:18 amatiphunzitsa ife kuti *"Kukula mu chisomo ndi chizindikiritso cha Ambuye wathu."*

- Kotero, ine ndinena kwa inu kuti ine ndakhala mu utumiki uwu kwa zaka zambiri, monganso inu amene mukuwerenga ichi kwa nthawi yoyamba, kuti bukhu ili lidzapereka kuwala kwakukulu ku "Bukhu la Chivumbulutso" kusiyana ndi mauthenga anga akale amene inu mukhoza kukhala nawo, kaya pa tepi, kulembedwa mwa bukhu, kapena zolemba zanuzanu pa zimene mlembi anapereka, kaya zaka 45 zapitazo kaya zaka 5 zapitazo.

- Ichi ndikunena, chifukwa mzimu womwewo wa Chivumbulutso umene unamupangitsa Yohane kulemba Bukhu la Chivumbulutso wapangitsa kuti limasuliridwe pano mu nthawi yotsiriza kwa Mkwatibwi Wake.

Izi ndikulankhula mokhudzana ndi bukhu lonse la Chivumbulutso, ndipo silinapangidwe pa cholinga chochotsapo vumbulutso lililonse limene Mulungu akanapereka patsogolo kwa ine kapena wina aliyense wa atumiki woona wa Mulungu pa Bukhu la Chivumbulutso. Inu mukhoza kukhala otsimikizika kuti vumbulutso lenileni silidzatsutsana ndi zolemba izi.

Posachedwa, utumiki onse woona udzaoneka diso kwa diso [1 Akorinto 1:10] pa kumasulira uku pamene liwu la vumbulutso la Mulungu liyamba kulankhula kuchokera kumwamba mu kufotokoza kwakukulu mwa Mzimu Wake [Chivumbulutso 10:8] pa zinthu zimene mukufuna muwerenge.

Ndikupempheni inu owerenga, kuti muzindikire kuti zolembedwa izi ndi za okhawo amene ali ndi makutu auzimu kuti amve chimene Khristu akunena kwa mkwatibwi wake pamene Iye akupanga chikondi ndi iye, chifukwa Bukhu la Chivumbulutso ndi kalata wa chikondi wa Mulungu kwa Mkwatibwi.

Kotero, mukatha kuwerenga bukhu ili, ngati silingadzutse wamkati wanu ndi kuwalira moyo wanu, ndiye pepani potenga nthawi yanu, ndipo chonde perekani bukhu ili kwa wina aliyense chifukwa chowaganizira mwa pemphero, mwina ndi lawo. Ine ndikukuthokozani mokoma chifukwa cha nthawi yanu ndi mgwirizano.

Pemphero langa kwa inu owerenga ndi ili: *Mulungu akupatseni inu mzimu wa mzeru ndi chidziwitso, ndi kuti maso akumvetsa kwanu awunikiridwe. Kuti mukamvetse masamba otsatira a bukhu ili. Bukhu ili likuthandizeni kuti muvale chovala choyera [Chivumbulutso 19:7-9], kuti musandulike mkazi wa Khristu pokhala m'modzi ndi Mau Ake munthawi yotsiriza iyi. Amen.*

Kuthokoza Kwapadera Kwa …

Ine ndikufunanso ndiwonetsere kuyamikira kwanga pa
ntchito
ya malemu William M.Branham mneneri wa Mulungu
wam'thenga
wa m'badwo uno wa Laodikaya komanso malemu mtumwi
Raymond M. Jackson
amene Mulungu anamugwiritsa ntchito kuti apitirize ntchito Yake imene Iye anaiyamba kupyolera mwa William Branham; makamaka mu gawo la mbiri la bukhu ili. Ngakhale ife sitili othandizidwa, kapena kukwezedwa ndi otsatira a
aliyense
wa uthenga wa amuna amenewa; zolemba zawo zinali zothandiza kwambiri pokonza bukhu ili.

Komanso, kuthokoza kwa padera kwa

Joyce Howard
Gary Gentry
Wanda Robertson
Barbara Howard
Leah Farruggia
ndi Enoch Kamanula

chifukwa cha kuthandiza mosatopa pa ntchito iyi.

"Ndipo anadza m'modzi mwa angelo asanu ndi awiri akukhala nazo mbale zisanu ndi ziwiri,
Nalankhula ndi ine, nanena, Idza kuno, ndidzakuonetsera iwe…"
Chivumbulutso 17:1.

Lemba la pamwambali likuonetsa m'modzi mwa angelo asanu ndi awiri amene akulankhulidwa kudutsa mu bukhu lonse la Chivumbulutso. M'modzi wa iwo akumuonetsa Yohane, amene akuimirira utumiki ngakhalenso kuimirira mkwatibwi, bukhu la Chivumbulutso. Kuona angelo asanu ndi awiri ndi kumvetsa ntchito zawo zimene iwo amachita ndi zinthu zopindula ku kumvetsa kwanu ku bukhu la Chivumbulutso. Izi zatsimikizidwa mu bukhu lonseli ngati chifungulo chenicheni chotsekula zinsinsi za [zoyamba] bukhu lozwizwitsa la Chivumbulutso.

.

MALONJE KU CHAPUTALA CHILICHONSE

Chaputala Chachinai

Chaputala chachinai chikuonetsera Yohane, woimirira mpingo woona, pamene iye akutengedwa kupita kumwamba mu Mzimu. Komanso chikuonetsera kuti mibado ya mpingo ikatha Mkwatibwi adzakwatulidwa kuchoka pa dziko pamene chisautso chikuchitika pano pa dziko. Yohane anaona Yesu atakhala pa mpando wa chifumu wa Atate. Iye anaona zamoyo zinai ndi akulu makumi awiri mphambu anai atakhala pa mipando yachifumu ing'ono ing'ono. Kodi zikutanthauza chiyani? Zafotokozedwa mu chaputala chachinai cha bukhu ili.

Chaputala Chachisanu

Chaputala chachisanu chikuonetsera Yesu atakhala pa mpando wa chifumu wa Atate ndi bukhu mu dzanja lake la manja losindikizidwa ndi zisindikizo zisanu ndi ziwiri. Yohane adakali mu masomphenya awa ndipo akuona Yesu atakhala pa mpando wa chifumu, anaona Mwanawankhosa akubwera ndikutenga bukhu kuchoka kwa Iye wakukhala pa mpando wa chifumu. Iye wokhala pa mpando wa chifumu wa Atate ndi Yesu, monga mphamvu ya moyo wosatha [Atate] yaikizidwa mwa munthu Khristu Yesu. Kotero Yesu ali pa malo a Atate mu masomphenya awa. Izi zikutanthauza kuti chinachake chimayenera kuonetsera Yesu akufunsa chimene Iye anachiombora. Kotero Mulungu anamulora Yohane kuona Mwanawankhosa mu masomphenya awa okhala ndi maso asanu ndi awiri komanso nyanga zisanu ndi ziwiri. Palibe cholengedwa chonga chimenecho kumwamba, zikungoonetsera chimene Yesu anatenga posandulika Mwanawankhosa wa Mulungu pamene Iye anafa pa mtanda.

Maso asanu ndi awiri komanso nyanga zisanu ndi ziwiri zikuonetsa ntchito zisanu ndi ziwiri za Mwanawankhosa mu mibado isanu ndi iwiri ya mpingo. Mwanawankhosa uyu akutenga bukhu mu dzanja la manja la Iye wokhala pa mpando wa chifumu.

Chaputala Chachisanu ndi chimodzi

Chaputala chachisanu ndi chimodzi chikuonetsera Mwanawankhosa akutsegula chisindikizo chachisanu ndi chimodzi mwa zisanu ndi ziwiri zimene zinali pa bukhu iye atatenga bukhu. Chaputala chachisanu ndi chitatu, vesi loyamba likuonetsa chisindikizo chachisanu ndi chiwiri chikutsegulidwa, chimene chinatsegulidwanso panthawi yotsegula zisindikizo zisanu ndi chimodzi zimene zalembedwa mu chaputala cha chisanu ndi chimodzi. Izi zinachitika mu 1963 pamene Mwanawankhosa amatsegula zisindikizo ndi kutumiza vumbulutso la izo ku Mpingo Wake mwa wam'thenga wa m'bado wa mpingo wachisanu ndi chiwiri.

Chaputala Chachisanu ndi chiwiri

Chaputala chachisanu ndi chiwiri chikuonetsera uthenga ukubwerera ku Israeli ndi Ayuda 144,000 akusindikizidwa ndi chisindikizo cha Mulungu. Chikuonetseranso khamu lalikulu limene linatuluka mu chisautso chachikulu ndi kutsuka mwinjiro yawo ndikuipanga iyo yoyera mu mwazi wa

Mwanawankhosa. Awa ndi anamwali opusa ndi iwo otulutsidwa mu mabungwe a zipembedzo mu gawo lotsiriza la zaka zitatu ndi theka za sabata la 70 la Danieli ndi 144,000. Choncho anamwali opusa amene anadzuka kumayambiriro a sabata, pamodzi ndi iwo anatulutsidwa mu zaka zitatu ndi theka zotsiriza ndi 144,000, pamodzi akupanga oyeramtima a kuchisautso.
Palibe njira iliyonse tingamvetsere chaputala ichi tisanamvetse koyamba kuti pali zaka zisanu ndi ziwiri zotsalira ku Israeli. Imeneyo ndi sabata la 70 la Danieli. Choncho izi zafotokozedwa ku mayambiriro kwa chaputala chachisanu ndi chiwiri. 144,000 akuitanidwa mu zaka zitatu ndi theka zoyambirira ndipo akulalikira uthenga wosatha mu zaka zitatu ndi theka zotsiriza, pamene oyera akuchisautso akupereka miyoyo yawo chifukwa cha kaimidwe kawo ndi Mau.

Chaputala Chachisanu ndi chitatu

Chaputala chachisanu ndi chitatu chikuonetsera, koyambirira, chisindikizo chachisanu ndi chiwiri chikutsegulidwa ndi Mwanawankhosa, izi zafotokozedwa mu chaputala cha khumi cha bukhu ili, ndipo ndizochitika za chisindikizo chachisanu ndi chiwiri.

Mu chaputala ichi, angelo asanu ndi awiri akupatsidwa malipenga asanu ndi awiri. Anai aiwo akuomba mu chaputala chachisanu ndi chitatu ndipo ndi uthenga wa aneneri awiri aku Chivumbulutso chaputala cha khumi ndi chimodzi. Izi zikuchitika mu gawo loyambirira la sabata la 70 la Danieli. Komanso, mngelo akulengeza miriri itatu imene ikuchitika pakati pa sabata.

CHIVUMBULUTSO CHAPUTALA CHACHINAI

Ngakhale chaputala chachinai ichi chikuonetsera choimirira cha Mkwatulo, ichi sichoimirira choyambirira chimene chikuonetseredwa apa, koma chimene chimene chikuonetseredwa apa ndi Mkwatibwi akutengedwa mu Mzimu wa vumbulutso iye atatulutsidwa mu m'bado wotsiriza wa mpingo, ndi Khristu, amene akuonetseredwa kunja kwa m'bado wa Laodikaya uwu. [Chivumbulutso 3:20]

Vesi 1*: "Zitatha izi ndinapenya, ndipo taonani, khomo lotseguka m'Mwamba, ndipo mau oyamba ndinawamva, ngati lipenga lakulankhula ndi ine, anati, Kwera kuno, ndipo ndidzakuonetsa zimene ziyenera kuchitika m'tsogolomo."*

M'bado wa Laodikaya ukangotha, kenako pali chitseko chotseguka chachikulu kwa Mkwatibwi, ndipo Khristu akuyamba kumuonetsa Mkwatibwi zinthu zakumwamba. **Apa ndi pamene tili mu nthawi.** Ife tili mu nthawi imene Mulungu akutsegula chitseko. Iye akutsegula chitseko kwa ndani? Osati kwa mabungwe, koma kwa Mkwatibwi wa Khristu.

Mulungu tsopano akutsegula chitseko kwa Mkwatibwi woona. Ichi ndi chitseko cha kwa Mkwatibwi, kumubweretsa iye ku ungwiro wathunthu. Zikupitirira kuoneka zazikulu zonse zimene Mulungu adzachita pa nthawi iyi, ndipo zikudziwika mu tsiku ili mu utumiki wa Chivumbulutso 10:8-11, umene ndi utumiki wobwezeretsedwa wa pa Aefeso 4:11.

Liu ili linayamba kulankhula ndi Yohane. Liu ili la lipenga ndi Liu la Ambuye Yesu Khristu. Pali maitanidwe amene akuperekedwa mu nthawi ino ku Mpingo, kwa Mkwatibwi weniweni wa Khristu, kwa iwo amene ndi owomboledwa, kwa iwo amene athawa mkwiyo wa zipembedzo. **Maitanidwe amenewo ndi oti "kwerani pamwamba pang'ono."** Liu la "lipenga" ndi gawo lotsiriza la utumiki wa Khristu, pamene Iye akutsika ku dziko monga zalembedwa ku 1 Atesalonika chaputala chachinai, vesi 16 ndi 17…, tiyeni tiwerenge. *"Pakuti Ambuye adzatsika kumwamba mwini yekha ndi mpfuu, ndi mau a mngelo wamkulu, ndi lipenga la Mulungu; **ndipo** akufa mwa Ambuye adzayamba kuuka. Pamenepo ife okhala*

ndi moyo, otsalafe, tidzakwatulidwa nawo pamodzi m'mitambo kukakumana ndi Ambuye mumlengalenga, ndipo potero tidzakhala ndi Ambuye nthawi zonse."

Taonani, pali magawo atatu [kapena maonekedwe] a Liu. Choyambirira pali **"Mpfuu,"** gawo la Liu. Izi zinayamba nkhondo yachiwiri ya dziko lonse la pansi itangotha chapakati mu ma 40, pamene Mulungu anayamba kubwezeretsa mpingo wake ku Mau a pachiyambi ndi chitsitsimutso cha machiritso akulu motsogoleredwa ndi malemu William Branham, pamene iye anatenga moto wa chitsitsimutso kuzungulira dziko lapansi kasanu ndi kawiri "mu nthawi ya mpfuu." Pamene tipitirira mu Mau ndi Mzimu, mpfuu umasandulika "Liu la Mngelo Wankulu," ndipo limasandulika kuomba kotsiriza [kapena lipenga] la Mulungu, ndipo izi ndi zimene Yohane anaziona mu mzimu pamene anatengedwa. Iliyonse ya magawo amenewa amamangika mu zinazo, kufikira pamene tifika ku gawo la lipenga, tili ndi chonse. Zonse zamangika mu chimodzi. Chitsanzo cha zimenezo…, ndi pamene Mulungu anabwezeretsa dongosolo la chiombolo. Pansi pa uthenga wa Lutera, zinali kuti "Olungama adzakhala ndi moyo mwa chikhulupiriro," kenako pansi pa Yohane Wesile kuyeretsedwa kunabwezeretsedwa; kenako mu 1906, ubatizo wa Mzimu Woyera unabwezeretsedwa. Apa tikhoza kuona kusiyana pakati pa magawo atatu a chipulumutso pamene chimabwezeretsedwa, koma tsopano, ndizoti landirani Yesu Khristu ndi kubatizidwa mu Dzina Lake, monga zinariri pa tsiku la Pentekosite.., **chochitika chimodzi, osati mu magawo atatu.** Ndi m'mene ziriri ndi Yohane, pamene iye akumva kulankhula kwa lipenga, chinali chochitika chimodzi. Ngakhale mu kubwezeretsa kwa Mulungu kwa ichi, Iye anachita izi mu magawo atatu [kapena maonekedwe..., mpfuu, liu la mngelo wankulu ndi kuomba kwa Mulungu.] Choncho pamene lipenga lirira, magawo awiri enawo akumvekanso. Chochitika chimodzi, kumveka kwa lipenga. Paulo adalankhula za chochitika chimodzi ichi, **"Taonani, ndikuuzani chinsinsi; sitidzagona tonse, koma tonse tidzasandulika, m'kamphindi, m'kutwanima kwa diso, pa lipenga lotsiriza** [kapena lipenga]**: pakuti lipenga lidzalira, ndipo akufa adzaukitsidwa osavunda, ndipo ife tidzasandulika."** [1 Akorinto 15:51-52]

Taonani apa mu kuomba kwa lipenga, uthenga ukudzutsa akufa ndi kusintha amoyo. Zikupangitsa kuchitika zonse zimene Paulo analemba za pano mu 1 Akorinto 15:51-52 ndi 1 Atesalonika, chaputala 4:16-17. Paulo anasiyanitsa magawo akubwera kwake mu 1 Atesalonika, koma anaziika izo palimodzi ngati chochitika chimodzi mu 1 Akorinto. Chimene chikuonetsera poyera kuti magawo atatu akubwera kwake ndi uthenga zakutiridwa mu kuomba kwa lipenga **lotsiriza.** Umenewo ndi uthenga wa Chivumbulutso, chaputala 10:8-11; chimene ndi kukwaniritsidwa kwathunthu kwa Aefeso 4:11-16. Potsiriza kwake udzaukitsa akufa ndi kusintha miyoyo. Izi zikuchitika Mkwatibwi atatulutsidwa mu m'bado wa chisanu ndi chiwiri ndipo akuima ndi Khristu, osati kachitidwe ka mpingo.

Tsopano mu kubwezeretsa kwa izi, Mulungu anagwiritsa ntchito koyambirira malemu William Branham, wam'thenga wa ku m'bado wachisanu ndi chiwiri, ndiye kenako mtumwi wofanana ndi Petro, amene anali malemu Raymond M. Jackson amene anabweretsa vumbulutso lina lakubwera kwake, tsopano zonse zakutiridwa mu uthenga wa Aefeso, chaputala chachinai, pamodzi ndi utsogoleri wa utumwi.

Nditalankhula izi, tiyeni tipitirire ndi Chivumbulutso chaputala chachinai vesi lachiwiri.

Vesi 2: *"Pomwepo ndinakhala mu Mzimu; ndipo taonani padaikika mpando wachifumu m' mwamba ndi pa mpandopo wadakhala wina."*

Pamene mukuwerenga uthenga uwu, inu mukhoza kutengedwa; inu mukhoza kutengedwa mu malo a mwambamwamba. Kenako inu mukhoza kumvetsa Bukhu la Chivumbulutso pamene ilo likumasulidwa.

Ine ndikufuna ndiwerenge mu chaputala choyamba cha Aefeso, vesi 15-20. Uyu ndi Paulo kulankhula ku mpingo. Ine ndikufuna ndikuonetsereni m'mene inu mungathe kutengedwera. Mavesi awa akuti, *"Mwa ichi inenso, m'mene ndamva za za chikhulupiriro cha mwa Ambuye Yesu chiri mwa inu, chimenenso mufikitsira oyeramtima onse, sindileka kuyamika chifukwa cha inu, ndikumbukira inu m'mapemphero anga; kuti Mulungu wa Ambuye wathu Yesu Khristu, Atate wa ulemerero, akupatseni inu* ***mzimu wa mzeru, ndi wa vumbulutso*** *kuti mukamzindikire Iye; ndiko kunena kuti* ***maso a mitima yanu awalitsike,*** *kuti mukadziwe inu chiyembekezo cha kuitana kwake nchiyani; chiyaninso chuma cha*

ulemerero wa cholowa chache mwa oyeramtima, ndi chiyani ukulu woposa wa mphamvu yache yolimba, imene inachititsa mwa Khristu, m'mene anamuukitsa kwa akufa, namkhazikitsa pa dzanja lake la manja m'zakumwamba."

Mulungu sanakuitaneni inu kuti mudzidyera mu zodyera nkhumba palimodzi ndi nkhumba kapena kukhala mu makola a nkhumba, koma Iye anakuitanani inu kuti mukhale oposa ogonjetsi. Iye anakuitanani inu kuti mutengedwe mu malo a mwamba mwamba, kuti mutengedwe mu Mzimu wa Ambuye, ndipo Iye adzakupatsani inu Mzimu wa kumvetsa.

Mulungu anagwira ntchito mwa Khristu pamene Iye anamudzutsa Iye kwakufa, ndipo ife tili gawo la ntchito imeneyo. Iye akufuna akupatseni inu Mzimu wa mzeru ndi Mzimu wa kumvetsa. Iye akufuna akupatseni inu mankhwala opaka m'maso. Mulungu anati Iye adzapereka ku mpingo mankhwala opaka m'maso mu masiku otsiriza. Kodi mankhwala opaka m'maso ndi chiyani? **Ndi mzimu wa mzeru, mzimu wa kumvetsa, mzimu wa chidziwitso, zili zoti zitengedwe mu malo a mwambamwamba ndi Khristu Yesu kuti mukamvetse zinthu zonse zimene Mulungu waziika kwa Mkwatibwi mu nthawi iyi.**

Taonani kuti Yohane sanatengedwe mu thupi. Ife tikuyenera kuchotsa maso athu mu thupi ndikuwapereka kwa Ambuye Yesu. Ife tikuyenera kuika maso athu pa munthu wamkati; chifukwa munthu wankati ameneyo ndi yekhayo amene angatengedwe mu malo a mwambamwamba mpakana thupi ili litasinthidwa mu kamphindi, mu kutwanima kwa diso. Mulungu akufuna kutenga munthu wankati, inu weniweniyo, ndikukuikani inu mu malo amwambamwamba mwa Yesu mu vumbulutso la Mau. Ichi ndi chimene anachita kwa Yohane.

Panali mpando wa chifumu utakhala kumwamba. Kumbukirani kuti lonjezo la kwa ogonjetsa ndi lakuti inu *"mudzakhala ndi Ine pa mpando wanga wa chifumu, monganso ine ndinalakika ndipo ndinakhala pansi ndi Atate anga pa mpando wake wachifumu."* [Chivumbulutso 3:21]

*"Ndipo panali **m'modzi** amene anakhala pa mpando."* Kodi Yohane adaona angati, a utatu inu? Kodi adaona angati, inu amene mumakhulupirira kuti alipo atatu mu Umulungu? Iye adaona m'modzi, osati awiri kapena atatu. Pamene iye adatengedwa kupita kumwamba ndikuona mpando wa chifumu, iye adaona m'modzi amene anakhala pa mpando wa chifumu. Ameneyu anali ndani? Iye anali Ambuye Yesu Khristu ndi ulamuliro wa Mulungu wa mphamvu utaikizidwa mwa Iye. **Mulungu anaikiza ulamuliro mwa Yesu Khristu ndi kumupanga Iye mutu wa mpingo.** Chifukwa chiyani Mulungu anaikiza izi mwa Yesu Khristu? Ndi chifukwa chakuti analakika.

Vesi 3: *"Ndipo maonekedwe a Iye wokhalapo anafanana ndi mwala wa jaspi, ndi sardiyo; ndipo panali utawaleza wozinga mpando wachifumu, maonekedwe ake ngati smaragido."*

Izi zikuonetsa mphamvu yonse ya Mulungu imene Iye anaikiza mwa Yesu. Utawaleza pa mpando wa chifumu ukuonetsera pangano. Mulungu anapanga pangano ndi munthu ndipo Iye anakwaniritsa izi kupyolera mwa Yesu Khristu. Apa Yesu akuoneka ngati waikidwa ufumu pa mpando wa chifumu wa Atate.

Vesi 4: *"Ndipo pozinga mpando wa chifumu mipando ya chifumu makumi awiri mphambu inai; ndipo pa mipandoyo padakhala akulu makumi awiri mphambu anai atavala zovala zoyera, ndi pa mitu pawo akorona agolide."*

Chonde khalani ndi chithunzi mu malingaliro anu a mpando wa chifumu ndi Yesu atakhala pa mpando wachifumu, ndipo pozungulira mpando wachifumu timipando makumi awiri ndi inai ndi akulu akulu atakhala pa timipando timeneti. Kodi akuluakulu amenewa ndi ndani? Akulu akulu amenewa akuimirira makolo khumi ndi awiri ndi atumwi a chiyuda a Mwanawankhosa khumi ndi awiri. Izi zikuimirira khoma ndi mazipata za mzinda wa ku Chivumbulutso, chaputala 21 ndi 22, koma tiyeni tiyembekeze ndipo tiwerenga kumeneko.

Mulungu anayamba kupereka ulamuliro wake ku chipangano chakale. Iye anayamba dongosolo lake kudzera mwa Abraham, Isake, ndi Yakobo, kenako akulu khumi ndi awiri, ndikumatsika. Ulamuliro

sikuti unali kwa akulu aku Chipangano chakale okha kapena kwa atumwi achiyuda khumi ndi awiri a Mwanawankhosa. Ichi ndi chithunzi chimene Yohane adachiona pamene iye anatengedwa mu Mzimu. Mu zoona zake, Yohane ndi m'modzi wa akulu amenewo.

Yohane adaona mpando wa chifumu waukulu, Yesu atakhala pa mpando wa chifumu, ndi utawaleza utazungulira mpandowo. Yesu anaikidwa pa udindo waukulu, ndipo pansi pake makolo khumi ndi awiri, ndi pansi pake atumwi khumi ndi awiri a Mwanawankhosa. Masomphenya a Yohane anaima pa ichi, koma kenako Mulungu anatenganso lingaliro lomwelonso pa Chivumbulutso 20:4. Akuti *"Ndipo ndinaona mipando yachifumu, ndipo anakhala pomwepo; ndipo ndinawapatsa chiweruzo."* [Kuweruza kunapatsidwa kwa iwo] Izi zikuonetsera Mkwatibwi wa Amitundu pamene Iye akubwera pamodzi ndi Khristu.

Tsopano chiweruzo ichi cha pa Chivumbulutso chaputala 20:4 chaikizidwa mwa ndani? Mkwatibwi wa Yesu Khristu. **Uku ndi kupitiriza kwa ulamuliro wa Mulungu kuupereka kwa Amitundu, mu gawo la Mkwatibwi.** Izi sizinali kwa akulu khumi ndi awiri kapena kwa atumwi khumi ndi awiri. Mau akuti ku 1 Akorinto 6:2-3, Paulo kulembera ku Akorinto [mongotchula] - "Kodi inu simungathe kuweruza timilandu tating'ono pakati panu? Kodi simukudziwa kuti oyeramtima adzaweruza dziko lapansi ngakhale angelo?" Izi zikuonetsera ulamuliro wa Mulungu kuperekedwa.

Pali chifungulo pa Chivumbulutso 3:21 pamene Yesu anati Iye walakika ndikukhala pansi ndi Atate ake pa mpando Wake wa Chifumu, ndi kuti yense wolakika adzakhala ndi Ine mu mpando wanga wachifumu. Izi sizikutanthauza kuti ife tidzayenda ndikupita ku mpando wa chifumu ndi kunena, "Choka Yesu kuti nafenso tikhale nawo pa mpando wa chifumu." Ayi, koma izi zikuonetsera ulamuliro wake ukupita mu mpingo wake mu Mileniamu, pamene ife tidzakhala mozungulira dziko kuweruza ndi kuphunzitsa anthu. Uwu ndi ulamuliro wa Mulungu ukuperekedwa kwa ogonjetsa. Izi zikutanthauza kuti Ulamuliro Wake waperekedwa pa dziko lonse. Mulungu amazionetsera izi kwa Yohane. Ndipo ndi zoti zidziwike mu tsiku ili ndi utumiki wa Mulungu.

Tsopano akulu makumi awiri mphambu anai awa anali ndi akorona a golide pa mitu yawo. Kodi akorona awa akuimirira chiyani? **Akuimirira a korona a ulamuliro.** Iwo anavekedwa. Iwo anapatsidwa malo [Mateyu 19:27-28], ndipo korona wa ulamuliro amangopitirira; koma Iye amapereka kwa oyeramtima ake. [Daniel 7:27] Mulungu anamulora Yohane kuona izi kuti ife tikadziwe mu nthawi iyi chimene Mulumgu akufuna kuchita.

Vesi 5: *"Ndipo mu mpando wa chifumu munatuluka mphenzi ndi mau ndi mabingu. Ndipo panali nyali zisanu ndi ziwiri za moto zoyaka ku mpando wa chifumu, ndiyo mizimu isanu ndi iwiri ya Mulungu."*

Chinthu chomwechi chinachitika pa phiri la Sinai pamene Mulungu anatsika, koma pa phiri la Sinai pamene mabingu ndi mphenzi zinamveka, anthu anachita mantha, koma pano, tikuona chifundo chitakhala pakati pa mpando wachifumu, munthu wosatchuka wa ku Nazarete, munthu amene Mulungu anaikiza ulamuliro wake onse, ichi chinapanga kusiyana. Ma liu a pa vesi lachisanu akuonetsa kuti vumbulutso lililonse limene limachokera kwa Mulungu limayambira pa mpando wa chifumu.

Uwu ndi mpando wa chifumu wa chifundo ngakhale pali mabingu ndi mphenzi zimene zikuonetsera Mzimu Waukulu Wamuyaya, Yehova Mulungu, koma simonga ku Chipangano Chakale. **Uyu ndi Mulungu- munthu, Yesu Khristu. Iye akhoza tsopano kumverera zosowa zathu ndi kuonetsera chifundo pa ife.** [Ahebri 5:1-6]

Tayang'anani, komanso, *"panali nyali zisanu ndi ziwiri za moto zoyaka ku mpando wachifumu, ndiyo Mizimu isanu ndi iwiri ya Mulungu."* Mizimu isanu ndi iwiri ya Mulungu imeneyo ikutchulidwa pafupi pafupi mu bukhu la Chivumbulutso, ngakhale Paulo mwini sanayambepo waitchula.

Mu chaputala choyamba cha Chivumbulutso, Yesu amayenda pakati pa choikapo nyali zisanu ndi ziwiri zimene zimaimirira mibado isanu ndi iwiri. Mizimu isanu ndi iwiri mu mibado isanu ndi iwiri ndi angelo asanu ndi awiri. Mu m'bado wina uliwonse nyali imayatsidwa ndipo imayakira m'bado umenewo, ndipo kenako ina imayatsidwa, mpakana pano tikuona nyali zonse zoyatsidwa; kuonetsera kuti pa ichi mibado isanu ndi iwiri ya mpingo yonse yatha.

Ku Chipangano Chakale kunali choikapo nyali zisanu ndi ziwiri mu kachisi kuwalira mkate. Wansembe amatenga moto wapachiyambi pa guwa umene umachokera kwa Mulungu ndi kuyatsa nyali yoyamba ndipo kuchokera ku yoyamba, zina zonse zisanu ndi imodzi zimayaka. **Taonani ichi, moto unachokera kwa Mulungu ndipo unagwa pa tsiku la Pentekosite. Zaka makumi awiri zoyambirira, moto unagwa pa guwa, ndi zokoma bwanji! Moto unagwa pa guwa ndikuyaka kwa nthawi zaka makumi awiri kuchokera mu 33A.D. mpaka 53A.D. Kenako moto unatengedwa pa guwa usanazime, ndipo nyali inayatsidwa. Nyali iyi inayaka kwa zaka zambiri mu m'bado wa mpingo woyamba, ndipo ina inayatsidwa ndipo inayaka kwa zaka zambiri mu m'bado wa mpingo wachiwiri, ndi zina zotero, mpakana mibado isanu ndi iwiri ya mpingo yatha tsopano, imene nyali zisanu ndi ziwiri za moto zikuimirira.**

Izi ndi zimene Yohane anaziona mu mzimu ngakhale kuti mwathupi iye sanachoke pa chisumbu cha Patmo mu masomphenya ake. Iye anangokhala mu mzimu ndi kutenga vumbulutso. Ichi ndi chimene Yohane anachiona ndipo ine ndikukuuzani vumbulutso la icho.

Vesi 6: *"Ndipo ku mpandowo, ngati nyanja yamandala yonga krustalo; ndi pakati pa mpandowo, ndi pozinga mpandowo, zamoyo zinai zodzala ndi maso kutsogolo ndi kumbuyo."*

"Nyanja ya mandala yonga krustalo" iyi ikutanthauza china chake. Iyo ikufotokozedwanso mu chaputala chakhumi ndi chisanu cha bukhu la Chivumbulutso, ndipo apo ili kuyaka ndi moto. Mu chaputala chakhumi ndi chisanu ife tikuona oyeramtima amene atenga chigonjetso pa chirombo, iwo amene anaphedwa mu nthawi ya chisautso, ataima apo pa nyanja ya mandala kuyaka moto.

Pa chaputala chachinai apa, nyanja ya mandala ikuonetsera njira yakumpando wachifumu ndipo kuli chifundo. **Kukhala ngati krustalo zikuonetsera kuti simukuyenera kudutsa mu chisautso kuti mupeze Yesu kapena kulowa mu ufumu wa Mulungu, tsopano njira [nyanja ya mandala] ili ngati krustalo, koma idzafika tsiku limene inu mudzayenera kudutsa mu moto kuti mupulumutsidwe,** monga ziriri mu chaputala chakhumi ndi chisanu cha bukhu ili.

Komanso, zamoyo zinai izi mu vesi lachisanu ndi chimodzi ndi zodzaza ndi maso. Kodi zamoyo zinai izi ndi chiyani? Ndi alonda oyang'anira njira ya kumtengo wa moyo. Iwo alankhulidwa mu Baibulo kuyambira ku Genesis, pamene a kerubi anaikidwa mu Edeni ndi lupanga loyaka [Genesis 3:24] akutetezera Adamu ndi Eva kudya za mtengo wa moyo mu maonekedwe a kugwa. Kotero zamoyo zinai izi zimayang'anira njira ya kumtengo wa moyo. **Poimirira, zimatetezera zinthu zodetsedwa kuti zisatchinge mpando wa chifumu wa Mulungu ndi kutenga moyo wamuyaya.** Sikuti pali chinachake chodetsedwa kumwamba, izi zalembedwa kwa ife pano pa dziko.

Izi zafaniziridwa ku chaputala chachiwiri cha Numeri, kumene zikuonetseredwa m'mene mafuko khumi ndi awiri a ana a Israeli anasonkhana, ndipo anali mu dongosolo la uzimu. Fuko lililonse mwa mafuko atatu linali ndi chikwangwani pamene panali chofanana ndi mkango, ng'ombe, munthu ndi chiombankhanga chouluka. Aliyense wa asilikali awa amayenera kumenyera ndi kufa kutetezera likasa la pangano asanalore wina aliyense kulowa mu kachisi mumene likasa la pangano linali. Ife tiona izi mochuluka mu chaputala 21 cha bukhu ili.

Kotero, sikungoti wina aliyense amabwera ndikuyang'ana mu Likasa la Pangano. Osati wongolimbira ndipo **osati munthu wa chipembedzo wina ali yense angayesetse kudutsa ndi kubwera ku vumbulutso ili la Mau a Mulungu. Pali oyang'anira, ndiye inu mukuyenera kudzera njira ya Mulungu.**

Maso kutsogolo komanso mbali zikuonetsa kuti inu mukuyenera kubwera njira ya Mulungu, [Machitidwe 2:38] ngati simutero, inu simungadutse alonda amenewo mu nthawi ino pamene Mulungu akuulura choonadi chake chonse cha Mau Ake.

Vesi 7: *"Ndipo chamoyo choyamba chinafanana nawo mkango, ndi chamoyo chachiwiri chinafanana ndi mwana wa ng'ombe, ndi chamoyo chachitatu chinali nayo nkhope yache ngati ya munthu, ndi chamoyo chachinai chinafanana ndi chiombankhanga chouluka."*

Zamoyo izi ndi zofunika kwambiri. Izo zimayang'anira ndi kutulutsa onse amene sakufuna kubwera njira ya Mulungu, koma zimatsegula njira kwa iwo amene akufuna kubwera mwa Mau. Inu mukabwera mwa mwazi, mwa utumiki usanu ndi kumva Mau, **ndiye inu mukhoza kudutsa alonda amenewo kupita ku mpando wachifundo,** umene ndi mpando wachifumu umene Yesu akukhalapo.

Iwo anakhulupirira chiphunzitso cha atumwi mu bukhu la Machitidwe. Chovuta ndi chiyani kukhulupirira chiphunzitso cha atumwi ndi kudutsa alonda amenewa kukafika pa mtima wa Mulungu, mu mpando wa chifumu wa Mulungu, ndikubwera ku zimene Mulungu akuchita lero? Ichi ndi chithunzi chimene chikuonetsera chimene chikuchitika lero mu mzimu.

Pamene Yesu Khristu anabwera pa dziko, panali olemba mauthenga anai: Mateyu, Marko, Luka ndi Yohane. Iwo anali alonda amene anayang'anira bukhu la Machitidwe kumene Khristu anaikidwa pa mpando wa chifumu m'mitima ya okhulupirira. Bukhu la Mateyu likuimirira mkango, bukhu la Marko, ng'ombe; bukhu la Luka, munthu, ndipo Yohane akuimirira chiombankhanga chouluka wokhala ndi zolemba za ulosi. Ife tafika apa pa izi chifukwa cha khalidwe la kalembedwe ka aliyense wa iwo.

Mateyu anali ngati mkango. Iye anapita mu vumbulutso lakuya kutionetsera m'mene Yesu anabadwira ndi ubatizo wa m'madzi. Ichi ndicho chifukwa ambiri amatenga Mateyu 28:19 ndipo samavomera Machitidwe 2:38, koma Mateyu anali mlonda, ndipo Mateyu 28:19 ndi chimodzimodzi Machitidwe 2:38.

Anthu ambiri sangathe kutenga chimene mlonda uyu akunena kuti, *"Chifukwa chache mukani, phunzitsani anthu a mitundu yonse, ndikuwabatiza iwo m'dzina la Atate, ndi la Mwana, ndi la Mzimu Woyera."* Iwo basi amangotchona pomwepo ndipo sangathe kumudutsa mlonda, koma pamene iwo ayang'ana mu vumbulutso la chimene Mateyu 28:19 akutanthauza, sangakhale ndi vuto ndi Machitidwe 2:38. Iwo amayenda kupitirira alonda ndikubatizidwa mu dzina la Yesu Khristu. Uwu ndi mkango kuyang'anira bukhu la Machitidwe.

Mbali imodzi ikuyang'aniridwa ndi mafuko atatu chakumpoto, chomwechonso kumwera, kum'mawa, ndi kumadzulo. Inu mukhoza kuzipeza izi ku Numeri chaputala chachiwiri. Koma apa, dongosolo la Mulungu la chipulumutso likuyang'aniridwa kutetezera iwo amene akufuna kubwera kwa Mulungu ndi ziphunzitso za mpingo wawo, zimene zimakana Mau monga atumwi anabweretsera.

Vesi 8: *"Ndipo zamoyo zinai, chonse pa chokha chinali nao mapiko asanu ndi limodzi; ndipo zinadzala ndi maso pozinga ponse ndi mkatimo; ndipo sizipumula usana ndi usiku, ndi kunena, Woyera, woyera, woyera, Ambuye Mulungu Wamphamvuyonse, amene anali, amene ali, ndi amene alinkudza."*

Zamoyo izi zimalemekezanso Mulungu usiku ndi usana ndipo zimazindikira chidzalo cha Mulungu mwa Yesu Khristu. Chidzalo cha Mulungu mu thupi ndi mwa Yesu Khristu, chifukwa amamutcha Iye apa *"Ambuye Mulungu Wamphamvu yonse, amene anali ndi amene ali ndi amene alinkudza."* **Iwo amazindikira kuti zinaikizidwa mwa Yesu Khristu kuti agwire ntchito malo awa.**

Vesi 9: *"Ndipo pamene zamoyo zipereka ulemelero ndi ulemu ndi mayamiko kwa Iye wakukhala pa mpando wa chifumu, kwa Iye wakukhala ndi moyo kufikira nthawi za nthawi;"*

Vesi 10: *"Akulu makumi awiri mphambu anai amagwa pansi pamaso pa Iye wakukhala pa mpando wa wachifumu, namlambira Iye amene akhala ndi moyo kufikira nthawi za nthawi, ndipo aponya pansi akorona awo ku mpando wachifumu, ndi kunena;"*[Akulu makumi awiri mphambu anai ndi makolo khumi ndi awiri, komanso atumwi khumi ndi awiri aku Israeli.]

Vesi 11: *"Muyenera inu, Ambuye wathu, ndi Mulungu wathu, kulandira ulemerero ndi ulemu ndi mphamvu; chifukwa mudalenga zonse, ndipo mwa chifuniro chanu zinakhala, nizilengedwa."* Taonani akulu akulu makumi awiri mphambu anai awa. **Inu simungathe kuwauza iwo kuti pali anthu atatu mu Umulungu. Apa pali chifukwa chake: Iwo anali ndi vumbulutso. Atumwi a Mwana wankhosa anali ndi vumbulutso. Akulu akuchipangano chakale anali ndi vumbulutso.** Palibe m'modzi wa iwo amene amakhulupirira mu milungu itatu. Iwo amaponya akorona awo pansi pa mpando wa chifumu. Izi zikuonetsera m'mene amamverera kudzichepetsa pa udindo umenewu. Iwo amati Ambuye ndi yekhayo amene anali woyenera, ndikuti iwo sanali woyenera pa udindo umene Iye anawapatsa iwo. Lero anthu ambiri amafuna kumadzikuza, chifukwa chakuti Mulungu awapatsa kaudindo kakang'ono. Koma tiyeni

tiyang'ane pa akulu akulu awa ndiye tilore iwo akhale chitsanzo chathu cha kudzichepetsa. Ichi chinali chithunzithunzi. Yohane anaona izi, koma chenichenicho iye ndi m'modzi wa akuluakulu, pokhala m'modzi wa atumwi khumi ndi awiri.

Kodi chaputala chachinai cha bukhu la Chivumbulutso ndi chiyani? Ndi choimirira mkwatulo, koma koyambirira chikuonetsa chitseko chotseguka kwa Mkwatibwi kuti atenge vumbulutso. Ichi chikuonetsera Khristu atakhala pa mpando wachifumu. Ichi chikuonetsera m'mene tingabwerere kwa Khristu ndi m'mene tingabwerere molondora. Chikuonetsera zamoyo zinai, alonda, amene amayang'anira njira ya kumtengo wa moyo ndipo palibe chimene chingafike pokha pokha chitabwera mu njira ya Mulungu.

Taonaninso, kuti panali m'modzi pa mpando wa chifumu, nyanja ya mandala inali yowala, kuonetsera kuti inu mukhoza kubwera kwa Khristu, koma mukuyenera kubwera njira yolondora.

Panali akulu akulu makumi awiri mphambu anai, kuonetsera kuti Mulungu amapereka ulamuliro wake kupyolera mwa munthu. Iye anapereka ulamuliro wake kuchokera mwa Khristu kutsika kwa anthu pamene iwo akuzionetsera wokha okhulupirika mu moyo uwu. **Nyali zisanu ndi ziwiri zikuyaka kuonetsera moto umene wayatsidwa ku m'bado wa mpingo uliwonse,** zikuonetseranso ntchito zisanu ndi ziwiri za Mzimu wa Mulungu mu dongosolo la chiombolo. Amen.

CHIVUMBULUTSO CHAPUTALA CHACHISANU

Vesi 1: *"Ndipo ndinaona m'dzanja la manja la Iye wakukhala pa mpando wa chifumu bukhu lolembedwa m'kati ndi kunja kwache, losindikiza ndi zisindikizo zisanu ndi ziwiri."*

Pamene tikuwerenga vesi loyamba, pali zinthu zina zimene zikumveka kwa ife. Choyamba, ife tikuona iye amene ali pa mpando wachifumu ali ndi bukhu [lofunyulura] mu dzanja lake lamanja, ndipo **"lalembedwa mkati."** Izi zikutiuza ife kuti chili chonse chomwe chinalembedwa kale masomphenya awa asanakhale. Ndiye ife tikuona kuti yasindikizidwa ndi zisindikizo zisanu ndi ziwiri. Izi zikutilora ife kudziwa kuti chili chonse chomwe chili mu bukhu ili sichikugwiritsidwanso ntchito yake koma ikusungidwa mudzanja lamanja la Khristu [okhala pa mpando wa chifumu wa Mulungu ngati Mulungu] mpakana nthawi yake yoti ikhalebe yosindikizidwa itatha. Ife tsopano tikhoza kuona tsopano kuti bukhu ili ndi lofunika kwambiri, ndipo aliyense amakhala ndi chidwi ndi kuyamba kudabwa pa zimene zalembedwa m'bukhuli…, ife zoona tikufuna kudziwa. Ichi ndiye cholinga cha izo kulembedwa ndi kuoneka mwa njira iyi. Ndi kubweretsa ludzu m'kati pa chimene chikuyenera kuuluridwa kwa Mkwatibwi Wake. Choncho ndi malingaliro amenewo, tiyeni tiyan'gane kwa Mulungu kuti tikhale ndi vumbulutso la icho, pamene Iye tsopano watsegula zisindikizo zisanu ndi ziwiri kwa ife kupyolera mwa Mwanawankhosa komanso mneneri Wake wa mu m'bado uno. Pamene tikumvetsa kuti "zisindikizo zisanu ndi ziwiri" zatsegulidwa kwa ife, tsopano tikhoza kukhala ndi mfundo zokwanira za bukhu lotsegula pamene likuperekedwa kwa ife ndi Mngelo Wamkulu wa pa Chivumbulutso, chaputala chakhumi.

Tsopano, tiyeni tiyan'gane pa chaputala ichi chachisanu mu kuona uku. Mpando wa chifumu uwu tione kuti Khristu walalika monga Chivumbulutso chaputala 3, vesi 21 chikuonetsera. Iye anachita izi pogonjetsa mayesero omwe mdierekezi amaponya pa Iye. Komanso, Iye anayesedwa mu zonse monga ife tili, komabe anali wokhulupirika mu zochitika zonse. [Ahebri 2:9-18].

Apa tikuona kusiyana pakati pa Adamu ndi Khristu. Chifukwa pamene Adamu anayesedwa, iye anagwa ku yesero ndi kutaya udindo, koma Khristu analakika ndi kutenga bukhu. Ichi ndi chimene chikuoneka pamene Mwanawankhosa akutenga bukhu kuchokera mu dzanja la manja la Atate patsogolo pake mu chaputala ichi.

Kotero pamene Adamu anataya ichi udindo ndi utsogoleri, zinabwerera kwa mwini wa pachiyambi amene anali Mulungu ndipo panalibe wina amene akanatha kuzitenga, kufikira Khristu anabwera ndi

kukwaniritsa chimene Mulungu anaika kuti munthu akathenso kuzitenga. Pamene chaputala ichi chikuonetsera, Khristu kukwaniritsa chimene Mulungu anaika ku kubwezeretsa kwa udindo uwu. Khristu anakwaniritsa ndipo anapatsidwa mphamvu ndi ulamuliro kuti atenge "zonse" zimene Adamu anataya m'munda mwa Edeni. Ndi bukhu lalin'gono mu dzanja lake la manja limene ndi ulamuliro wa Mulungu kuperekedwa ku mtundu wa anthu. Iye anaupereka ku mpingo pa tsiku la Pentekosite [Machitidwe, chaputala 2], chimene chinali kwa Ayuda kutenga anthu pakati pa Israeli anthu odzalamulira ndi Iye mu nthawi ya mileniamu. Koma, pamene mayesero anabwera, mpingo wa chiyuda unagwa kuyesero ndi kusankha lamulo pamwamba pa chisomo, pamene iwo amasaka chilungamo mwa ntchito [Aroma 10:3-4], m'malo moti achilandire ndi chikhulupiriro mwa Khristu. M'mene anachita izi, Mulungu anawapangitsa khungu, kuti Iye akatenge anthu kuchokera kwa Amitundu chifukwa cha Dzina Lake kapena kuti akhale Mkwatibwi Wake. [Machitidwe 15:14]

Tsopano, apa ndi pamene kabukhu kakan'gono kakubwera mu chithunzi **chosindikizidwa ndi zisindikizo zisanu ndi ziwiri.** Ichi ndi chimene Mulungu anampatsa Adamu ndipo iye anachitaya ichi. Kenaka Iye anachipereka kwa Khristu ndipo Iye anachipereka kwa abale, Ayuda anachitaya ichi. Kenaka Khristu anapereka ulamuliro kwa bwenzi lake kapena Mkwatibwi wake ndikuwapatsa iwo mtumwi Paulo kuwalangiza iwo m'mene iwo angamukondweretsere Mkwati. Izi zikumveka bwino pa chimene Khristu anamuuza Paulo pamene iye anagwa pansi ndi kuwala kwakukulu panjira yaku Damasiko [Machitidwe 9:15], kumuuza Paulo kuti Iye adzamutumiza kwa Amitundu. Patsogolo pake mu utumiki, Paulo analemba ku Aroma 11:13, "Ine ndine mtumwi kwa Amitundu." Kenaka iye anayamba kulemba kwa Amitundu makalata amalangizo, kuwalimbikitsa ndi kuwadzudzula m'mene iwo angakondweretsere Mkwati; koma iwo amazikonda zonse iwo asanagwe ku yesero ndi kutaya kabukhu kakan'gono. Kenaka Mulungu anaulora mpingo kulowa mu mibado isanu ndi iwiri ya mpingo ndi makalata amene Paulo adawalembera. Chimene chinachitika chinali chakuti…, Mulungu anachotsa kumvetsa kwa Mau ndi kusindikiza ndi zisindikizo zisanu ndi ziwiri. Njira yokhayo mpingo unalandirira vumbulutso kwa icho, inali kudzera mwa angelo asanu ndi awiri auzimu ndi amithenga a mibado isanu ndi iwiri, pamene m'bado wa mpingo uliwonse unabwera mukudutsa kwa nthawi.

Choncho mu nthawi imeneyo, Mulungu anachotsa gawo la uzimu, kapena mphamvu yopangitsa gawolo kukhala moyo ndikulisindikiza kunja kwa mibado isanu ndi iwiri ya mpingo koma anasiya malangizo mu maonekedwe a zolembedwa. Kotero, kumvetsa kwa uzimu kwathunthu sikunapatsidwa kwa anthu pafupifupi kwa zaka zikwi ziwiri. Chitsanzo cha chimene Mulungu anachita potenga gawo lauzimu kuchotsa mu bukhu…. m'munda mwa Edeni, Iye anachotsa Mzimu wa Edeni, koma anasiya malo a nthaka. Izo zinathetsa paradaizo, chifukwa Mzimu wa paradaizo unachotsedwa koma osati malo ayi Palibe ngakhale mchenga umodzi umene unapita pamodzi ndi Mzimu wa Edeni; udakali pompano lero. Chimene ine ndikukuonetserani inu apa ndi chakuti palibe ngakhale mau amodzi wolembedwa a malangizo a Paulo amene anachotsedwa pamodzi ndi kabukhu kakan'gono. Mulungu anangochotsa kumvetsa kwa uzimu mu makalata a Paulo ndipo sizimadziwika, pokhapokha zitaloredwa kuti zitero ndi angelo auzimu asanu ndi awiri pamene iwo amatumikira kupyolera mwa amithenga asanu ndi awiri a pansi, pamene Khristu amatumikira ngati Wansembe Wamkulu. Izi zaonetseredwa ku Chivumbulutso, chaputala chakhumi.

Pamene mpingo unagwa kuchoka ku Mau enieni, ndi kumvetsa kokha kumene kunachotsedwa koma osati Mau olembedwa. Kumvetsa kunasindikizidwira kunja kwa mibado isanu ndi iwiri ya mpingo. Apo ife tili ndi zisindikizo zisanu ndi ziwiri pa bukhu. Zisindikizo zimabisa ulendo umene mpingo unadutsamo mu kagawo ka nthawi monga zakambidwa ku Mateyu, chaputala 13 mu mafanizo asanu ndi awiri ngati m'bado wa ufumu wa kumwamba, chimene ndi mibado isanu ndi iwiri ya mpingo. Kotero pamene kabukhu kakan'gono kakutengedwa ndi Mwanawankhosa mu chaputala ichi, ndi zisindikizo zikuchotsedwa zikutsiriza "chinsinsi" cha m'bado uno, chimene chatsirizidwa ndi wam'thenga wa m'bado wa chisanu ndi chiwiri [mngelo] monga Chivumbulutso 10:7 chikuonetsera poyera. Pamene zisindikizo zisanu ndi ziwiri zinatsegulidwa kumwamba ndikutumizidwa padziko ndi mwa kubangula

kwa mabingu asanu ndi awiri kupyolera mu liu la wam'thenga wa m'bado wa chisanu ndi chiwiri, izi zachitika kale monga chaputala cha 10 cha bukhu ili chikuonetsera.

Tsopano ife tikuona Yesu akukhala pa malo pa Atate. Mulungu amafuna chinachake kuti chichitike chimene chikanaonetsera chimene Yesu anatenga posandulika Mwanawankhosa wa Mulungu. Ichi ndi chifukwa chake mu chaputala ichi, tikuona Mwanawankhosa akubwera ndikutenga bukhu m'manja mwa Iye amene akhala pa mpando wachifumu. Izi zikuonetsera Yesu Khristu kutenga ulamuliro wa Mulungu Wamuyaya umene Iye anatenga posandulika Mwanawankhosa wa Mulungu pa dziko, koma poti dziko linalephera, Yesu amayenera kukhala pamenepo ngati m'khala pakati kwa zaka zikwi ziwiri pamene mibado ya mpingo imayenda.

Yesu Khristu anali kukhala pa mpando wachifumu kuimirira Mulungu, ndipo Mulungu anali ndi bukhu. Panalibe munthu amene anali woyenera, koma mu masomphenya, Mwanawankhosa anabwera ndikutenga bukhu. Kodi mukuona chifukwa chake chimene panalibe munthu amene anapezeka woyenera kutsegula bukhu? Ndi chifukwa chakuti aliyense anabadwa mu tchimo la kusakhulupirira.

Kotero, palibe ngakhale m'modzi kuchokera ku mbewu ya Adamu amene akanatha kutenga bukhu. Atapita Adamu, aliyense anabadwa mu kusakhulupirira ndipo sakanatha kuchita icho. Kenako Yesu anabwera. Iye anali yani? Iye anali mbewu ya Mulungu.

Ine ndikufuna inu muone chifukwa chiyani zinatengera kubadwa mwa namwali. Ichi ndi chofunika. **Palibe wina aliyense wobadwa mu mtundu wa Adamu amene akanatha kutenga cholowa cha Adamu.** Osati Eliya, osati Davide, palibe m'modzi wa iwo, koma apo panabwera m'modzi amene anabadwa mwa Mulungu. Baibulo likuti Yesu Khristu anabadwa osati mwa chifuniro cha thupi, koma cha Mulungu. Iye sanali mbewu ya Adamu. Iye anali mbewu ya Mulungu, ndiye kotero, Iye anali nao angwiro, magazi osadetsedwa akuthamanga m'mitsempha yake.

Namwali Maria anati, *"Kukhale kwa ine monga mwa mau anu."* Iye anakhala ndi pakati. Mwa chiyani? Osati mwa mwamuna aliyense, koma Mulungu kumuphimba iye, **ndipo pamene mwana ameneyo anabadwa, apo panali M'modzi amene akanatha kutenga bukhu.** Baibulo likuti *"Iye amene sanachite tchimo, ndipo mkamwa mwache sichinapezedwa chinyengo"* [1 Petro 2:22]. Kodi ichi chikutanthauza chiyani? Iye nthawi zonse anakhulupirira Mau a Mulungu.

Vesi 2: *"Ndipo ndinaona mngelo wamphamvu wakulalikira ndi mau akulu, ayenera ndani kutsegula bukhu, ndi kumasula zisindikizo zake?"*

Zikutanthauza chiyani pamene akuti iye adaona mngelo "wamphamvu?" Zikutanthauza kuti akuika ndemanga pa bukhu. Zili chimodzimodzi ngati ndikanakulemberani inu kalata ndiye ndikufuna kuika mfundo yaikulu; Ine ndikadayiunikira iyo. Kotero Yohane adaona "mngelo wamphamvu" chifukwa kufunika kunaikidwa mu bukhu mu masomphenya.

Mngelo anafuula ndi mau akulu. Yohane anadziwa kuti bukhulo linali lofunika, iye anadziwa kuti wina wake amayenera kutsegula bukhu kupanda kutero, ife sitikatha kubwezeredwanso ku chimene Paulo analalikira

Muchaputala chachisanu ndi chimodzi cha bukhu ili inu mudzapeza kuti zisindikizo zimenezo zinatsegulidwa kwenikweni mu 1963, ndikutumizidwa ku dziko ndi Mwanawankhosa kupita kwa wam'thenga wa m'bado wa chisanu ndi chiwiri kuti ziuluridwe ku mpingo. Zikutanthauza chiyani? Zikutanthauza kuti nthawi yake ya Iye kufuna chiombolo chake inafika pachimake.

Vesi 3: *"Ndipo sanathe m'modzi mwamba kapena pa dziko, kapena pansi pa dziko kutsegula pa bukhupo, kapena kulipenya."*

Panalibe munthu amene akanayandikira kutenga bukhuli. Sakanatha kulitsegula, ngakhale kuyan'gana pa ilo.

Kodi mukutha kumvetsa chimene Yesu anachita pa mtanda tsopano? Posandulika Mwanawankhosa wa Mulungu, kodi mukhoza kugwira chimene Yesaya mneneri amatanthauza pamene iye anati ku Yesaya 53:7- *"Iye anatsenderezedwa koma anadzichepetsa yekha osatsekula pakamwa."* Kodi mukutha kuona chimene Iye anachita pamene anapfuula, *"Mulungu wanga, Mulungu wanga, mwandisiiranji ine?"* Iye

analavulidwa malovu, kumenyedwa, kudzudzulidwa, chisoti cha minga kuvekedwa pa mutu pake, ndipo minga zinaikidwa m'mutu mwake; koma Iye sanatsegule pakamwa pake. Chifukwa chiyani? Iye amatenga ulamuliro kuti atsegule bukhu, kuti awombole inu ndi ine. Iye anaombola mtundu wonse wa Adamu kuyambira ku munda wa Edeni kudutsa njira yonse. Muvi unalasa m'nthiti mwake ndipo madzi ndi mwazi zinatuluka. Iye anakhala akumva kupweteka pa mtanda kwa maora, ndipo anayesera kumpatsa Iye vinyo wosasa ndi ndulu zimene zikanatha kupha ululu, koma Iye anakana. Iye anamwa chikho chowawa. Iye anafa ngati Mwanawankhosa wa Mulungu pa phiri la Kavare.

Kodi mukutha kumuona Iye akumenyedwa, magazi akutsikirira pa Iye, kulavuliridwa malovu, ululu ndi kumva zowawa? Komabe Iye amayenera kutenga bukhu. Iye amayenera kuchita chinachake kuti atenge ulamuliro wotenga bukhu. Kodi mukutha kuona chimene Iye anachita m'munda ndi chimene anachita pa mtanda pamene Iye anati, "Kwatha?" Popereka moyo wake pa Kavare, Iye waombola mbewu yonse yodziwidwiratu ya Mulungu. Mbewu yonse ya Adamu imene idalephera, kuchimwira Mulungu, ndikuperewera mulemerero wa Mulungu, Iye anayiombola. Baibulo likuti Mulungu anaika pa Iye kusaweruzika kwa ife tonse. Iye anamenyedwa. Yesaya 53 akutionetsera ife zimene Iye anadutsamo kuti asandulike Mwanawankhosa, koma apa, Iye wakwezedwa ndipo akukhala mu mpando wa chifumu wa Mulungu. Munthu angakhalebe wochimwa bwanji ataona izi?

Vesi 4: *"Ndipo ndinalira kwambiri, chifukwa sanapezedwa m'modzi woyenera kutsegula bukhulo, kapena kulipenya."*

Inenso ndikanalira, inu simukanatero? Ngati nditadziwa kuti bukhu limenero silinafunsidwepo ndipo palibe aliyense amene anabweretsa zimene zinataika, chikanakhala chinachake cholirira.

Ife sitili mumaonekedwe athu alondora tsopano. Ndicho chifukwa ife timatopa nthawi zina. Chilengedwe chonse chimabuula ndipo ife timadziwa kuti sitili pa malo athu olondora, koma chiombolo chidzafunsidwa, dziko lidzafunsidwa, ndipo paradaizo wa Mulungu adzakhala pompano pa dziko lapansi.

Kotero, m'modzi wa akulu adalankhula ndi Yohane, ndipo anasiya kulira ndikuyamba kufuula Poona kuti chiombolo chafunsidwa.

Vesi 5: *"Ndipo m'modzi wa akulu ananena ndi ine, usalire: taona, Mkango wochokera mu pfuko la Yuda, muzu wa Davide, walakika kutsegula bukhu ndi zizindikiro zake zisanu ndi ziwiri."*

Mkango wa pfuko la Yuda ndi ndani? Ndi Yesu. Iye analakika mu zonse, ndipo ndi mkango wa Yuda. **Koma Iye sikuti akanatenga bukhu chifukwa chakuti anali ndi udindo wa "Mkango wa pfuko la Yuda." Ndi chifukwa chakuti anasandulika Mwanawankhosa.**

Yesu ndi Mfumu yathu, komabe ngakhale Iye anali Mfumu, izo sizinagule chiombolo. Kotero pamene Yohane anayang'ana, iye sanaone Mfumu ndipo sanaone Mkango. Iye anaona chiyani? Tayang'anani ichi. Apa pakubwera vumbulutso la icho.

Vesi 6: *"Ndinaona pakati pampando wa chifumu ndi zamoyo zinai, ndi pakati pa akulu, Mwanawankhosa ali chiriri ngati waphedwa; wokhala nazo nyanga zisanu ndi ziwiri, ndi maso asanu ndi awiri, ndiyo mizimu isanu ndi iwiri ya Mulungu, yotumidwa ilowe mu dziko lonse."*

Ine ndikukhulupirira kuti aliyense amene ali ndi Mzimu Woyera akhoza kuona ichi. Apa panabwera Mwanawankhosa ndi nyanga zisanu ndi ziwiri komanso maso asanu ndi awiri. **Choyamba zikuonetsa chimene Yesu anachita pa dziko pamene Iye anakhala Mwanawankhosa.** Chachiwiri, zikuonetsa kuti nyanga zisanu ndi ziwiri ndi maso asanu ndi awiri ndi angelo asanu ndi awiri amene anakhala gawo lalikulu la ntchito ya Mwanawankhosa mu mibado ya mpingo, mpakana kuti ife mu nthawi yotsiriza sitingakhoze kutenga vumbulutso loona la kachitidwe ka Mwanawankhosa tisanaone m'mene angelo asanu ndi awiri, kapena mizimu isanu ndi iwiri ya Mulungu, inaulurira Mwanawankhosa ku mibado isanu ndi iwiri ya mpingo. Izi zikumveka bwino mu chaputala cha khumi cha bukhu ili.

Taonani, uyu anali Mwanawankhosa amene anali ataphedwa. Pokhala ophedwa, anali ndi magazi. Izi zikuonetsera mwazi pa mpando wa chifundo kwa mibado isanu ndi iwiri ya mpingo.

Vesi 7: *"Ndipo anadza nalitenga bukhu ku dzanja la manja la Iye wakukhala pa mpando wa chifumu."*

Iye anabwera kudzafunsa chimene Iye adaombola. Ichi chikuchitika. Mu 1963, Mulungu adatsegula zisindikizo zisanu ndi ziwiri.

Mwanawankhosa uyu akubwera ndi kutenga bukhu. Izi sizimapanga anthu awiri mu masomphenya. Padakali munthu m'modzi mu masomphenya a Yohane. Mwanawankhosa uyu anali nawo maso asanu ndi awiri ndi nyanga zisanu ndi ziwiri. **Simunthu, zikungoonetsera ntchito imene inachitika pa dziko.**

Nyanga zisanu ndi ziwiri ndi maso asanu ndi awiri akuonetsera kuti kupyolera mwa mibado isanu ndi iwiri ya mpingo Iye anakhalabe Mwanawankhosa wa Mulungu. Mwazi wake unayeretsa ndi kuperekedwa kwa anthu ochimwa mu M'bado wa M'dima ndi kupitirira.

Apa ndi pamapeto pa m'bado pamene Iye akutenga bukhu, pamene mibado ya mpingo isanu ndi iwiri yatha. **Kwenikweni, nthawi yake yeniyeni ndi 1963 pamene izi zinayenba kuchitika.**

Vesi 8: *"Ndipo pamene adatenga bukhulo, zamoyo zinai ndi akulu makumi awiri mphambu anai anagwa pansi pamaso pa Mwanawankhosa, zonse zili nao azeze, ndi mbale zagolide zodzala ndi zofukiza, ndizo mapemphero a oyeramtima."*

Kumbukirani kuti izi zonse zili mumasomphenya. Yesu akukhala pa malo a Mulungu Wamuyaya. Iye analakika ndi kukhala pansi pa mpando wa chifumu wa Atate. Mwanawankhosa akuimirira Yesu Khristu mu masomphenya, kuonetsera ntchito ya udindo Wake. Kotero zamoyo izi ndi akulu amagwa pansi ndikuyamba kulambira Mwanawankhosa. Iwo ali ndi azeze ndi mbale zagolide zodzaza ndi zofukiza, ndizo mapemphero a oyeramtima. Palibe pemphero lopita pa chabe la oyeramtima limene linaperekedwa M'bado wa M'dima. Mapemphero onse a oyeramtima amene akhala akupemphera adakali mu malingaliro a Mulungu; choncho tipitirire kupemphera.

Vesi 9: *"Ndipo ayimba nyimbo yatsopano, ndi kunena, muyenera kulandira bukhulo, ndikumasula zisindikizo zache; chifukwa mwaphedwa, ndipo mwagulira Mulungu ndi mwazi Wanu anthu a mafuko onse, ndi manenedwe onse, ndi mitundu yonse."*

Pali chimwemwe chachikulu mwamba Iye asanabwere pa dziko, kusiya kumwamba kuli chete kwa theka la ora [Chivumbulutso 8:1] pamene Khristu ali pa dziko. [Chivubulutso 10].

Iye anali woyenera chifukwa Iye anaphedwa. Zikuonetsera kuti Iye anaphedwa pa dziko. Mwanawankhosa wa magazi akuimirira Yesu pamene Iye anapita pa mtanda.Yohane anali nako kumvetsa kwa izi. Akulu anali nako kumvetsa kwa izo.

Izi sizinafike ku gawo la Ayuda okha, koma zinafika ku dziko lonse lapansi, chifukwa akuti: *"Chifukwa mwaphedwa, mwagulira Mulungu ndi mwazi wanu anthu a mafuko onse, ndi manenedwe onse, ndi mitundu yonse."* Kachiwirinso, nyanga zisanu ndi ziwiri, ndi maso asanu ndi awiri akuimirira amithenga a mibado isanu ndi iwiri ya mpingo, ndi angelo auzimu asanu ndi awiri amene Khristu anagwiritsa ntchito mu nthawi ya nyengo ya mibado isanu ndi iwiri ya mpingo.

Pamene bukhu ili likutsegulidwa ndi kuperekedwa ku mpingo, [Chivumbulutso 10], ife sitikutenga dziko nthawi imeneyo, koma Mulungu akutipatsa ife nthawi yapamwamba mu dziko tsopano.

Vesi 10: *"Ndipo mudawayesa iwo ufumu ndi ansembe kwa Mulungu wathu; ndipo achita ufumu padziko."*

Ichi chikutanthauza chiyani? Zikutanthauza kuti mbewu ya Adamu yaomboledwanso, ndiye kotero Iye amatipanga ife olamulira a dziko ndi Iye. Kodi mukuziona tsopano? Izo zikuchitika posachedwapa; ndi nthawi ya ulamuliro wa mileniamu. Iye ndi Mulungu woombora. Mukuona chimene Iye watiombolera ife. Zonse zili mu bukhu.

Zonse zimene Mulungu ali nazo kwa Mkwatibwi zaonetseredwa ngati kuti zili mu bukhu: Ulamuliro, chidziwitso, mzeru, zipatso za mzimu ndi zina zotero; zonse zili mu bukhu. Kodi inu simuli okondwa kuti dzina lanu lili m'menemo? Icho ndi chenicheni.

Vesi 11: *"Ndipo ndinaona, ndipo ndinamva mau a angelo ambiri pozinga mpando wa chifumu, ndi zamoyo ndi akulu; ndipo mawerengedwe awo anali zikwi khumi kuchulukitsa zikwi khumi ndi zikwi za zikwi."*

Kodi mukutha kuona chimene zikutanthauza? Izi zikutsimikizira pa bukhu ndi amene akanalitenga. Angelo awa anayamba kuyamika Mwanawankhosa. Izi zikutanthauza kuti Iye amafunsa ulamuliro umene Mulungu anampatsa Iye, chifukwa ife sitingayamike chilichonse koma Mulungu. Iye ndi Mwanawankhosa, Iye ndi Mfumu, Iye ndi Mkwati, Iye ali chonse ichi. Yohane anamuona Iye mu masomphenya mu njira iyi, kotero ife tikhoza kuzitenga kupyora m'malingaliro athu auzimu zimene Mulungu akuchita. Kotero amayamba kuyamika Mulungu.

Vesi 12: *"Akunena ndi mau akulu, Ayenera Mwanawankhosa, wophedwayo, kulandira chilimbiko, ndi chuma ndi mzeru, ndi mphamvu, ndi ulemu, ndi ulemelero, ndi chiyamiko."*

Angelo zikwizikwi awa akuti *"Ayenera Mwanawankhosa amene anaphedwa."* Izo zikuyankha funso lakuti Mwanawankhosa ndi ndani. Iye analandira mphamvu chifukwa Iye anasandulika Mwanawankhosa osati chifukwa anali Mkango, koma chifukwa anasandulika Mwanawankhosa. Kodi izo sizopambana m'mene Mulungu akutenga masomphenya awa a Yohane ndikuwatanthauzira?

Kodi inu mukuzindikira kuti Yesu Khristu ali pakati pathu? Kodi inu mukuzindikira maudindo amene Mulungu waika mu mpingo kumasulira Mau kwa Mkwatibwi wa mu nthawi yotsiriza, kuti tikachotse zodetsa zonse ku minjiro yathu ndi kusinthika mukamphindi, mukuthwanima kwa diso kukakumana ndi Ambuye mlengalenga. Ine ndili okondwa kuti pali mtumwi oti atithandize kumvetsa izi.

Angelo anati, "Ayenera Mwanawankhosa amene anaphedwa, kulandira chilimbiko, chuma ndi mzeru, ndi mphamvu, ndi ulemu, ndi ulemerero ndi chiyamiko!"

Vesi 13: *"Ndipo cholengedwa chilichonse chiri mwamba, ndi padziko, ndi pansi pa dziko, ndi m'nyanja, ndi zonse zili momwemo, ndinazimva zili kunena, Kwa Iye wakukhala pa mpando wa chifumu, ndi kwa Mwanawankhosa zikhale chiyamiko, ndi ulemu, ndi ulemerero, ndi ufumu, kufikira nthawi za nthawi."*

Ndi chiyani? Ndi Chivumbulutso chaputala 5 chikumasuliridwa chikuonekera ku mpingo. Pamene Yohane anaona ichi, ndi chonse chimene akanatha kuima nacho. Iye amayenera kupfuula pang'ono. **Yohane anapeza vumbulutso lakuti Mwanawankhosa anali yani ndi chimene anali kukhala pa mpando wachifumu ndipo anadziwa kuti anali yemweyo mu maudindo osiyanasiyana.**

Vesi 14: *"Ndipo zamoyo zinai zinati, Amen. Ndipo akuluwo anagwa pansi nalambira Iye wokhala ku nthawi za nthawi."*

"Amen" amatanthauza *zikhale choncho.* Kodi mukuona chimene chili mu chaputala chachisanu cha bukhu la Chivumbulutso tsopano?

Mu bukhu la Danieli 7:13-14 likuti *"Ndinaona masomphenya a usiku, taonani, anadza ndi mitambo ya kumwamba wina ngati Mwana wa munthu, nafika kwa nkhalamba ya kale lomwe; ndipo anamuyandikitsa pa maso pache. Ndipo anampatsa ulamuliro, ndi ulemerero ndi ufumu, kuti anthu onse, ndi mitundu yonse ya anthu, ndi manenedwe onse, amtumikire; ulamuliro wache ndi ulamuliro wosatha ndi ufumu wake sudzaonongeka."* Awa anali masomphenya a Danieli a Yesu kutenga ulamuliro umene takhala tikuwerenga za iwo. Panthawi imene Danieli adamuona Iye, adamuona Iye ngati Mwana wa Mulungu, chifukwa Iye anali asanakwaniritse udindo wa Mwanawankhosa. Pa Danieli 7:18 akutinso *"Koma oyeramtima amwambamwamba adzalandira ufumuwo, ndikukhala nawo ufumu kosatha, ku nthawi zamuyaya."* Kodi Yohane anati chiyani? Iye anati watipanga ife mafumu ndi ansembe ndipo tidzalamulira dziko lapansi.

Kodi ndi udindo wandani kulamulira? Ndi udindo wa Khristu ndipo Iye anatipatsa ife ulamuliro kulamulira ndi Iye, koma izo sizidzakhala ku mbali iyi ya mileniamu ya Khristu. Mu mbali iyi ya mileniamu, Mulungu akufuna ife kuti mphamvu zimene zili mwa ife zifike ku ungwiro. [2 Petro 1]

Tangoganizani za Yesu kuvekedwa minga, kulavuliridwa, kunyozedwa, koma Iye anali nacho chipiriro, Iye anali ndi chidziletso. Zonse zimene Mulungu anaika mwa munthu zinali pa mayesero tsiku limenelo, koma Iye anatulukamo ogonjetsa. Ichi ndi chifukwa chake Iye adanena ku m'bado wa mpingo wotsiriza uwu, *"Ndikulangiza iwe kuti ugule kwa Ine golide woyengeka m'moto."* [Chivumbulutso 3:18] Kodi mukutha kuona kuti wayesedwa mu moto ndipo watuluka wangwiro! Ine ndikufuna chimene chayesedwa, inu simukufuna?

Potseka chaputala ichi Ine ndikufuna ndinene kuti masomphenya akupitirira apa, chifukwa akupitirira kukamba za Iye amene anakhala pa mpando wa chifumu ndi kwa Mwanawankhosa. Yohane adakali mu masomphenya omwewo ngakhale mu machaputala ena a bukhu la Chivumbutso. Zinampanga Yohane kukhutira kuwona Mwanawankhosa akubwera ndi kutenga bukhu. Ndipo mu chaputala chakhumi ndi chimodzi, Iye akuyamba kutsegula zisindikizo zisanu ndi ziwiri.

Mulungu atithandize ife tonse kuti timvetse ndilo pemphero langa. Amen.

CHIVUMBULUTSO CHAPUTALA CHACHISANU NDI CHIMODZI

Mu chaputala chachisanu ndi chimodzi, ife tikuyenera ndithu kubweretsa Mau m'mene alili lero. Chifukwa chiyani chake: Zisindikizo zimenezi zinatsegulidwa mu 1963 pamene Mulungu analankhula vumbulutso la izo kupyolera mwa wam'thenga wa m'bado wachisanu ndi chiwiri, William Branham. Kotero, izi zachitika kale mu utumiki wa m'bale Branham.

Mu chaputala cha chisanu cha chivumbulutso pali m'modzi atakhala pa mpando wa chifumu, ndi Mwanawankhosa wokhala ndi nyanga zisanu ndi ziwiri ndi maso asanu ndi awiri ndi kutenga bukhu mu dzanja la Iye amene akhala pa mpando wa chifumu. Izi sizikupangitsa kukhala anthu awiri mu UMulungu monga m'mene taphunzirira mu ma chaputala ambuyowa. Tayang'anani Mwanawankhosa akuoneka ngati ndi Iye amene ali ndi ulamuliro kumasula zisindikizo kumwamba, ndipo izi zikukwaniritsidwa mu zoimirira, sizikuchitika kwenikweni mpakana Khristu atabwera ngati Mngelo Wankulu ndipo pamodzi ndi Iye angelo auzimu asanu ndi awiri amene anali aku mibado isanu ndi iwiri ya mpingo. Umo ndi m'mene angelo asanu ndi awiri amenewo akadalankhula mu Chivumbulutso chaputala cha khumi, kupyolera mwa wam'thenga **wapansi** pano wachisanu ndi chiwiri kudzatsiriza "chinsinsi cha Mulungu," monga zinadziwikira mwa kulira kwa mabingu asanu ndi awiri kwa Mkwatibwi Wake, monga iye analandirira vumbulutso la chimene chinachitika mu masomphenya a Yohane a Mwanawankhosa kutsegula zisindikizo kumwamba. Tsopano zachitika mu nthawi yeniyeni, kuonekera pa dziko mu 1963, pamene zisindikizo zisanu ndi ziwiri zamasulidwa mu dziko, kupyolera mwa mneneri wa mu nthawi yotsiriza M'bale William Branham. Ichi chikupangitsa Chivumbulutso, chaputala cha khumi kukhala chooneka mwangwiro kwa Mkwatibwi wa Amitundu.

Chaputala chachinai, chachisanu, ndi chachisanu ndi chimodzi cha Chivumbulutso zimayendera limodzi ndipo lingaliro lomwelo lagwiridwa mu njira yonse, kuonetsera ulamuliro wa Mulungu ndi m'mene zikusamukira kupita ku Mpingo.

Vesi 1: *"Ndipo ndinaona pamene Mwanawankhosa anamasula chimodzi cha zizindikiro zisanu ndi ziwiri, ndipo ndinamva chimodzi mwa zamoyo zinai, nichinena, ngati mau a bingu, Idza."*

Pamene Mwanawankhosa anatsegula chisindikizo choyamba, chinthu choyamba chimene Yohane adaona chinali chimodzi cha zamoyo zinai chikuti, *"bwera udzaone,"* ndipo panali liu limene linamveka ngati bingu, bingu limodzi lobangula. Palibe kubangula kwa bingu pa kutsegulidwa kwa zisindikizo zina. Kodi izi zinachitika liti? Mwanawa nkhosa anayamba kutsegula zisindikizo pamene **angelo asanu ndi awiri anabwera kwa m'bale Branham mu 1963.** Panali kubangula kumodzi kwakukulu ndipo zisindikizo zisanu ndi ziwiri zinatsegulidwa kwa Mkwatibwi. "Bingu" limaonetsera liu la Mulungu kulankhula kwa wam'thenga wa m'bado wa mpingo.

Yohane anamva ichi ngati kulira kwa bingu, koma pa kuchitika kwenikweni kwa ichi ku Arizona panali kulira kwa bingu zimene zimaoneka ngati zimafuna kugwedeza phiri. Mwanawankhosa amatsegula zisindikizo kumwamba kuti azitumize izo ku dziko kupyolera mwa angelo asanu ndi awiri amene anaonekera kwa m'bale Branham mu 1963.

Zamoyo zinai izi ndizofunika mu chaputala chachisanu ndi chimodzi ndi kutsegulidwa kwa zisindikizo. Chimodzi mwa zamoyo zinai chinati, *"Bwera udzaone."*

Komanso, bukhu lofunyulura losindikizidwa ili lili ngati pepala lopindidwa limene lili ndi zomatira mozungulira ilo zisanu ndi ziwiri ndipo pambali pa zomatira polembedwa pang'ono. Mwa chitsanzo, pa chomatira choyamba akukamba zimene vesi ili lachiwiri lili.

Vesi 2: *"Ndipo ndinapenya, ndipo taonani, kavalo woyera, ndipo womkwerayo anali nawo uta; ndipo anampatsa korona; ndipo anatulukira wolakika kuti alakike."*

Izi zangolembedwa pa zomatira zimene zikumatulidwa, koma sizitsegula bukhu. Izi sizikutsegula ngakhale gawo limodzi la magawo asanu ndi awiri a bukhu. **Bukhu lidakali losindikizidwa mpakana chisindikizo chachisanu ndi chiwiri chimatulidwe.** Zisindikizo izi zatenga ulendo wonse wa mpingo kuyambira pa chiyambi mpakana ku mapeto.

Zamoyo zinai zimalengeza pa kutsegulidwa kwa chisindikizo zinai zoyambirira, ndipo ine ndikufuna inu muone m'mene zamoyo izi zikuonekera. Tiyeni tibwerere tikazitengenso zamoyo zinai zimenezi ku chaputala chachinai, vesi la chisanu ndi chiwiri. *"Ndipo chamoyo choyamba chinafanana nao mkango, ndi chamoyo chachiwiri chinafanana ndi mwana wa ng'ombe, ndi chamoyo chachitatu chinali nayo nkhope yake ngati munthu, ndi chamoyo chachinai chinafanana ndi chiombankhanga chakuuluka."* Ndizofunika m'mene zamoyo izi zikuonekera.

Pamene chisindikizo choyamba chinamasulidwa chamoyo choyamba chinati, *"Bwera udzaone."* Zamoyo izi zili mu dongosolo la m'mene zikugwiritsidwira ntchito mu mibado ya mpingo: mkango, ng'ombe, munthu, ndi chiombankhanga. Tayang'anani m'mene zalembedwera mu Mau chifukwa ndi momwemo m'mene izo zaikidwira mu mibado ya mpingo. Chimodzi mwa zamoyo zinai chinati, *"Bwera udzaone,"* pamene anamasula chisindikizo choyamba.

Tsopano gwirani ichi: chonse chimene Yohane anachiona chinali *"kavalo woyera, ndipo womukwerayo anali nawo uta; ndipo anampatsa korona; ndipo anatulukira wolakika kuti alakike."* Tayang'ani kuti pali akavalo anai mu chaputala chimenechi; kavalo woyera, kavalo wofiira, kavalo wakuda ndi kavalo wotumbuluka. Wokwera pa kavalo ndi m'modzi yemweyo. Chinthu chokhacho chimene iye akuchita ndi kusintha akavalo. Iye akuyamba ndi kavalo woyera, kenako kavalo wofiira, kenako kavalo wakuda ndipo potsiriza akutenga kavalo wotumbuluka, koma ndi wokwera kavalo m'modzi yemweyo nthawi yonse. Izi ndizofunika, pamene mudzakhala mukuziona.

Kodi wokwera kavalo ameneyu ndi ndani? Apa pali yankho. Pamene Khristu anakwera kumwamba mu maonekedwe a thupi, Iye anabwereranso mu maonekedwe a Mzimu Woyera ku dziko kudzagwira ntchito yake. Pamene anabwera, satana anaona kugwira ntchito kwa Mulungu mwa Mzimu Woyera ndi m'mene Mulungu anagwiritsira ntchito Mzimu Woyera kugwira ntchito ndi mpingo woyamba. Choncho satana anachita chiyani? **Iye anatumiza chofanizira ndi Mzimu Woyera.** [Gwirani ichi, chifukwa ndi chofunika njira yonse.] Iye anatumiza chofanizira ndi Mzimu Woyera weniweni, ndipo chofanizira pamene chinabwera chinali pafupifupi chenicheni. Mateyu 24:24 akuonetsa kuti mizimu imeneyo idzakala yofanana kwambiri kuti ngati ndi kotheka ikanyenge osankhidwa; koma sikotheka kunyenga osankhidwa, tithokoze Ambuye.

Tayang'anani ichi: pamene Mose anabwera poyera, panaonekanso Balamu. Mose anali mneneri woona wa Mulungu ndipo Balamu anali mneneri wabodza. Iwo onse ananenera, ndipo zonse zimene Mose ananenera zinachitika, koma zochepa za zomwe Balamu ananena zinachitika.

Pamene Yesu anabwera poyera, ndani amene anabwera poyera ngati chofanizira, ngati wotsutsakhristu? Yudasi Isikalioti. **Mizimu iwiri imeneyi yakhala ikuyenda mbali ndi mbali njira yonse.**

Yesu anapachikidwa, ndipo atadutsa mu nyumba yandende ya satana ndi kumasula andende kuwabweretsa iwo pamene iye anauka, [Mateyu 27] Iye anakwera kumwamba ndi kutumiza Mzimu wake.

Yudasi anadzipachika yekha ndikugwa pa malo otsetsereka, naphulika pakati, ndi matumbo ake onse anakhuthuka. [Machitidwe 1:18] Iye anadzipha yekha. Mzimu umene unali mwa Yudasi umene unali mzimu wa satana, mzimu wa otsutsakhristu, unabwera kudzatsutsa kugwira ntchito kwa Mzimu wa Mulungu.

Pakuyenera kukhala Khristu pasanakhale wotsutsakhristu. Mawu oti "Khristu, Messia," amatanthuza *odzozedwa.* "Wotsutsakhristu" amatanthauza *chinachake chomenyana ndi Khristu weniweni.* Ndi *mzimu wa chipembedzo,* osati chikominizimu.

Mu m'bado woyamba, satana anayamba kumenyana ndi ntchito ya Mulungu poyesera kulowa ndi kutenga anthu kuchoka pa Mau. Pamene Paulo analembera a Tesalonika, iye anati *"chinsinsi cha kusayeruzika chayambadi tsopano."* [2 Atesalonika 2:7] Kodi chinsinsi cha kusayeruzika ndi chiyani? Ndi mzimu wa otsutsakhristu. Kumbukirani kuti ndi mzimu wa chipembedzo, osati chikomunizimu kapena izimu wina aliyense.

Yohane analembera kwa mpingo ndikuti, *"Ana inu, ndi nthawi yotsiriza iyi; ndipo monga mudamva kuti wokana Khristu akudza, ndipo tsopano alipo wokana Khristu ambiri; mwa ichi tizindikira kuti ndi nthawi yotsiriza iyi."* [1 Yohane 2:18] Izi zikuonetsera kuti mzimu wa wotsutsakhristu unayamba kubwera kwa anthu mu m'bado woyamba ndipo udzakhala pa iwo pokhapokha ngati tirigu ndi nansongole zikukulira limodzi, ndipo zilekanitsidwa ku nthawi ya kumapeto.

Chenjezo lotsiriza la Paulo kwa akulu ku Aefeso linali…, kuti pali amuna **ali kale pakati panupakati,** ndipo ine ndikangopita iwo adzadzuka ndikudzitengera ophunzira a iwo eni. [Machitidwe 20:29-30] Mzimu umenewo wa wotsutsa Khristu umalowa mu mpingo. Kotero, pamene chisindikizo choyamba ichi chimatsegulidwa chikulankhula za kavalo woyera, ndipo iye amene anakwera pa iye anali ndi uta, ndipo anapita kugonjetsa ndi kugonjetsa. Ichi ndi chokhacho chisindikizo choyamba chikulankhula, koma kodi kumasulira kwake ndi kotani? Unali mzimu wa otsutsakhristu ukuyenda mu m'bado wa mpingo woyamba. Umawoneka ngati wabwino. Umaoneka bwino, koma kunali kugwira ntchito kwa satana.

Mzimu wa otsutsakhristu umagwira ntchito nthawi zonse kupyolera mwa malingaliro a chithupi thupi mwakufuna kupanga gulu losonkhana lokongola ndi kufuna kuika ma Edala, madikoni, mabishopi, mapapa, ndi ena otero, kuuchotsa mpingo ku utsogoleri wa Mulungu. Mulungu ali ndi utsogoleri wake ndipo uli mu komanso kupyolera mu utumiki usanu.

Kotero kavalo oyera ndi otsutsa khristu mu maonekedwe ake abwino oyera pamene anali mu mpingo wapachiyambi. Mwina mzimu wotsutsakhristu umatha kunena chinachake ngati, "Ife tikudziwa Paulo Woyera ndi munthu wabwino, ife sitikukaika zimenezo, ndipo ife sitinganene kuti Paulo sanali mtumwi, ife tikukhulupirira kuti iye ndi mtumwi; ***koma..."*** Apo pali kavalo woyera, wokwera kavalo wotsutsakhristu. Izi zili ndi moyo lero.

Oyeramtima anamufunsa Paulo nthawi ina za iwo amene anafa ndi kupita. Paulo anati, "Ine ndikuuzani m'mene zidzakhalire." Iye anati "*Akufa mwa Ambuye adzayamba kuuka; pamenepo ife okhala ndi moyo, otsalafe tidzakwatulidwa nawo pamodzi m'mitambo, kukakomana ndi Ambuye mumlengalenga."* [1 Atesalonika 4:16-17] Mzimu wotsutsakhristu unati, "Chabwino, ife tikukhulupirira kuti Paulo watenga vumbulutso, ndipo mu zonse Paulo akulondora, ***koma…"***

Mzimu wotsutsakhristu sukanatha kutembenuka ndi kunena kuti Paulo anali mdierekezi wakalekale ndipo musamumvere, umenewo sukanakhalanso mzimu wa mtundu woyera. Mzimu wa mtundu woyera udakali pano lero, mzimu wofiira udakali pano, mzimu wakuda udakali pano, ndi wotumbuluka [kapena waphulusa] udakali pano.

Mzimu wa mtundu woyera ukanati, "Inde, ife tikudziwa kuti Paulo ndi mtumwi, nanga bwanji mukutsutsana nazo izo? Pali amuna ena. Ife tili nawo Mzimu Woyera. Mzimu Woyera ukhozanso kulankhula nafe." Kodi mukuona m'mene zinalili? Mzimu umenewo ukanati, 'Ine ndikukhulupirira kuti padzakhala chiukitsiro, koma za kukwatulidwa, ine sindikudziwa. Paulo alibe lemba la zimenezo. Ife tikanazikhulupirira ngati iye akanakhala nalo lemba. Ndionetseni lemba." Kodi mukumuona kavalo woyera, mdierekezi wakaleyo? Iye adakali pano, koma mkangowo udakali panonso! **Mulungu anaika ulamuliro mu udindo wa utumwi ndipo iye sanauchotse. Udakali pompepo.** Izi sizikanagwira ntchito pamene mpingo unali mu maonekedwe ake akugwa mu mibado ya mpingo, koma tsopano tabwezeretsedwanso. Izi zikugwira ntchito lero. Utumiki onse woona umene ukutumikira pansi pa mzimu wa mkango. Wokwera kavalo woyera ameneyo akukweranso lero. Ali nawo onse akavalo anai ndipo

wina aliyense amene amamukhala ndi amene amalumphirapo. Inde, mdierekezi ali nazo zonse zamoyo zake, koma Mulungu ali nazonso zonse zake. Kwa oyeramtima okhala ndi vumbulutso, tili oposa agonjetsi.

Vesi 3: *"Ndipo pamene anamasula chisizindizo chachiwiri, ndinamva chamoyo chachiwiri nichinena, Idza udzaone."*

Vesi 4: *"Ndipo anatuluka kavalo wina wofiira: ndipo anampatsa iye womkwera mphamvu yakuchotsa mtendere pa dziko ndi kuti aphane; ndipo anampatsa iye lupanga lalikulu."*

Tayang'anani, okwera kavalo uyu analibe lupanga mu chisindikizo choyamba. Iye anali ndi korona ndi uta, koma iye analibe mivi yathupi, koma amangoponya mivi yauzimu yochuluka. Iye akuchita zimenezo lero. Iye sanali woti adzipha anthu. Wokwera kavalo woyamba ntchito yake inali kuchotsa anthu ku Mau a Mulungu pomaika chinachake mkati chimene sichinali cholondora, koma iye anaona kuti iye sakanatha kuwachotsa pa Mau chifukwa mzimu wa mkango umalonderera.

Chisindikizo ichi chachiwiri chinagwiranso ntchito mu mibado yoyambirira, koma chinsinsi chake sichinamasulidwe kufikira mu 1963. Wotsutsakhristu anatsika kavalo woyera ndikukwera kavalo wofiira, ndiye apo iye anapatsidwa lupanga lalikulu kuti aphe ndi lupanga ndikuchotsa mtendere padziko.

Kumbukirani kuchokera ku kuphunzira kwathu kwa mibado ya mpingo muchaputala chachiwiri ndi chachitatu; kuti mu m'bado wachiwiri ndi wachitatu wa mpingo Khristu anawauza kuti amadziwa ntchito zawo, ndi chilemetso chawo. Lonjezo ku mpingo wachiwiri linali, "Iye amene alakika sadzachitidwa choipa ndi imfa yachiwiri." Ichi chimaonetsa kuphedwa mu mpingo woyamba mu m'bado umenewo, ndipo chonse chimene akanachita ndi kuvutika chifukwa cha Ambuye. Chimene chikanawapangitsa kuchita zimenezo ndi chiyani? Kodi chamoyo chachiwiri chimene chinachoka kwa Mulungu chinali chiyani? Mzimu wa ng'ombe. Kodi mzimu wa ng'ombe ndi chiyani? Ndi nyama imene imagwira ntchito, ndipo ndi nyama ya msembe. Pamene Iye anakwera pa kavalo wofiira anayamba kuwapha, Mulungu anatumiza mzimu wa chamoyo chake chachiwiri pa mpingo, chamoyo chachiwiri chimene chinati "Bwera udzaone."

Aroma anawapha akhristu, zikwi zikwi mu m'bado uwu mpingo wa katolika wa chiroma usanabwere mu 300A.D. Kenako mpingo unapha. Zalankhulidwa ndi mngelo wa chisanu ndi chiwiri kuti Mpingo wa katolika wa chiroma unapha anthu mamilioni makumi asanu ndi limodzi kudza mphambu zisanu ndi zitatu. Anawapha iwo ndikupitirira kupha mpakana mu1500A.D. Panali nyengo ya zaka chikwi yotchedwa M'bado wa M'dima. Mpingo wa chiroma wa katolika utayambika, iwo amene samanyoza chikhristu chenicheni ndi kuvomereza chipembedzo chachikatolika amaphedwa. Analipo mamilioni a iwo.

Ngati inu mutati muwerenge mbiri zakale inu mudzaona kuti uyu anali wokwera kavalo wofiira amene akuchokera kwa mdierekezi. Ndi mzimu womwewo wa otsutsakhristu njira yonse. Mzimu wotsutsakhristu siunafike ku chidzalo mwa munthu m'modzi, koma udzatero kumapeto. Iye akukwera kavalo wofiira mu nthawi ya chisindikizo chachiwiri. Kumbukirani kuti chamoyo choyamba chinali mkango ndipo chachiwiri chinali ng'ombe. Pamene zamoyo zonse zinai zidzabwera pa dziko, mukudziwa chimene chidzakhale? Izo zidzakhala mozungulira mpando wachifumu monga momweYohane anazionera kumwamba. Mpando wa chifumu wa Mulungu udzakhalanso pa dziko mwauzimu monga mu bukhu la Machitidwe. Ulamuliro wa mpingo, bukhu, udzakhalanso padziko. Chisindikizo chachiwiri ndi kupitiriza kwa chisindikizo choyamba. Ndi mzimu womwewo.

Vesi 5: *"Ndipo pamene anamasula chizindikiro chachitatu, ndinamva chamoyochachitatu nichinena, Idza. Ndipo ndinapenya, taonani, kavalo wakuda ndipo iye womkwera anali nawo muyeso m'dzanja lake."*

Kodi chamoyo chachitatu chimene chinachokera kwa Mulungu chinali chiyani? Chamoyo chachitatu chinali nayo nkhope ngati munthu. Munthu ndiwodzisamala kuposa chamoyo chilichonse. Chamoyo chimenecho chinaimirira **mzeru ya munthu;** monga Lutera, Wesley, ndi ena.

Pa nthawi iyi anthu amakhulupirira kuti wamsembe anali nayo mphamvu kusandulitsa vinyu kukhala mwazi wa Yesu ndi kusandulitsa mkate kukhala thupi la Ambuye Yesu. Nthawi ina Lutera anali kunyamula m'gonero mu mpingo ndipo iwo anati, "Ili ndi thupi la Khristu ndipo uwu ndi mwazi wa Khristu." Lutera anaponya m'gonero pansi ndikunena, "Ili sithupi la Yesu Khristu ndipo uwu simwazi wa Khristu! Uwu ndi mkate ndi vinyo." Inu mukutha kuona kuti iyi ndi mzeru ya Mulungu ikubwera.

Wokwera pa kavalo wakuda uyu anali ndi muyeso mu dzanja lake. Iye ali wokonzeka kuyeza chinachake.

Vesi 6: "*Ndipo ndinamva ngati mau pakati pa zamoyo zinai, nanena, Muyeso wa tirigu wogula rupiya ndi miyeso itatu ya barele yogula rupiya; ndi mafuta ndi vinyo usaziipse."*

Ichi ndi chiphunzitso chachithupithupi cha wotsutsakhristu, chimene iye amagulitsa kupyolera ku mpingo wake wa chithupi thupi. Pa nthawi iyi zinali kupyorera mu mpingo wa ku Roma. Kenako, zinalinso kupyolera mwa achiprotestant. Mu M'bado wa M'dima mpingo wabodza uwu unayamba kugulitsa m'gonero. Anthu amayenera kulipira akamakwatirana; pamene mwana abadwa; amayeneranso kulipira kukakhala maliro; kuwapempherera kuti achoke ku pirigatore. Dziko linali mu m'dima waukulu umenewu kuyambira mu 500A.D. mpakana mu1500A.D. pamene kukonzanso kunayamba kubweretsanso kuwala kwa Mau.

Tayang'anani, ku mayambiriro, wokwera kavalo yemweyi anayamba ndi kavalo woyera ndi kuyesera kubwera mu mpingo ndi kuunyenga iwo. Iye anadzala mbewu, kachitidwe ka Chinikolai. Ndiye chinakhala chiphunzitso cha Chinikolai, ndi chiphunzitso cha Yezebeli, chiphunzitso cha Balamu, ndi zina zotero. Ndiye anapitirira ndi kupha iwo amene sanali mu mzere wa chiphunzitso chake. Pamene anapha iwo, dziko lonse linali mu m'dima.

Tayang'anani kavalo wakuda ameneyo, M'bado wa M'dima. Panali nyengo ya zaka chikwi pamene zimaoneka ngati dziko limabwerera mbuyo. Pa nthawi imene dziko limachoka mu m'bado wa m'dima, ufumu wa Aroma ndi mizinda yawo ya mutsiku limenelo inali italowa pansi. Ambiri anafa ndi miriri imene imachitika mu nthawi imeneyo. Matenda ndi umphawi zinali ponse ponse. Chinali chiyani? Anali satana kulamulira dziko kwa zaka chikwi ndi mkazi wake.

Nyengo ya zaka chikwi iyi ya m'dima imaimirira wotsutsakhristu akukwera kavalo wakuda kupyola mu M'bado wa M'dima. Mpingo wa katolika unayamba kugulitsa mapemphero ndi chiphunzitso chabodza; ndipo ndi chimene mpingo wakatolika ukuchita lero.

Pamene Kukonzanso kunayamba ndipo kuwala kochuluka kwa uthenga kunayamba kuunika, Roma sanathenso kulisunga dziko mu m'dima waukulu. Mukudziwa chifukwa chiyani? Kulikonse kumene kukonzanso kunapita, kuwala kwa Mau a Mulungu kunayamba kuunikira, ngakhale mu gawo la sayansi munthu anayamba kutukuka ndikutuluka mu umbuli ndi kupusa kwake. Pamene Kukonzanso kunayamba kuzungulira pa dziko lapansi, Roma sanathenso kusunga dziko lapansi mu m'dima; chirombo chinalandira chibala chachikulu. Zinali mwa mzeru ya munthu kuti Kukonzanso kunayambika. "Mzimu wa munthu," chinali chamoyo chimene chinabwera ndikutulutsa dziko lapansi ku M'bado wa M'dima.

Tayang'anani kuti gawo lotsiriza la vesi lachisanu ndi chimodzi likuti, "*ndi mafuta ndi vinyo usaziipse."* Kodi ichi chikuimirira chiyani? Ngakhale mu m'dima wa mu m'bado wa m'dima wochuluka panali kagulu kakang'ono ka oyeramtima woona amene anali ndi chimwemwe cha Ambuye ndi vumbulutso la Mau a Mulungu.

Liu ili limene linati, "*ndimafuta ndi vinyo usaziipse,"* zikutanthauza kuti sizikanatheka kuwaletsa. Iwo sakanatha kukhudza moyo uwo wa Mulungu. Iwo anapha mamilioni a zotengera koma moyo wa Mulungu unapitirira, vinyo ndi chimwemwe cha Mzimu Woyera. Iyi ndi mbiri.

Kumbukirani kuti kavalo wakuda uyu unali mzimu wa wotsutsakhristu kugulitsa chiphunzitso chake ndi m'gonero, ndikumanena kuti anali nayo mphamvu kusandulitsa vinyo kukhala magazi a Khristu ndi mkate kukhala thupi la Khristu. Koma Lutera, nkhope ya munthu, analemba mfundo 95 za zimene zinali zolakwika ndi mpingo wa Chikatolika wa Chiroma ndi kuika pa chitseko chakasitolo ku Wittenberg, Germany.

Lutera anakhudzidwa ndi ndale kuti apange nyengo ya dziko lapansi kukonzekera kuti mpingo ukhale ndi moyo ndi kukula. Mzeru ya munthu inachita zimenezo; chinali chinthu chokhacho akanachita. **Iye amayenera kuchita mu gawo la umunthu chifukwa sakanatha kuchita mu gawo la uzimu kwambiri, chifukwa mpingo siunali wauzimu**. Iwo samadziwa ngakhale kuti olungama adzakhala ndi moyo mwa chikhulupiriro. Uthenga wa Lutera unali, "Olungama adzakhala ndi moyo mwa chikhulupiriro."

Tsopano mu tsiku ili lotsiriza chiombankhanga chabwera. Uno ndi m'bado wa chiombankhanga. Chiombankhanga chimenecho ndi chiti? Ndi mzimu wa chamoyo chachinai kubwera ku dziko ndi kubweretsa vumbulutso. Mzimu wa chiombankhanga ndi umodzi mwa zamoyo zinai zimene zinali mozungulira mpando wachifumu wa Mulungu. M'bale Branham anali m'modzi mwa oyamba kutumikira pansi pa chikoka cha mzimu umenewo wa chiombankhanga. Chiombankhanga chimenecho chidakaulukabe, chifukwa vumbulutso la Mau a Mulungu likupitirirabe. Zonse zinai za zamoyo izi zidakali pompano.

Vesi 7: *"Ndipo pamene anamasula chizindikiro chachinai, ndinamva mau a chamoyo chachinai nichinena, Idza udzaone."*

Vesi 8: *"Ndipo ndinapenya, taonani, kavalo wotumbuluka; ndipo iye womkwera, dzina lake ndiye Imfa; ndipo Hade anatsatana naye; ndipo anawapatsa ulamuliro padera la chinai la dziko, kukapha ndi lupanga, ndi njala, ndi imfa, ndi zirombo za padziko"*

Choyambirira, wokwera kavalo uyu anakwera kavalo woyera, kenako anakwera kavalo wofiira, kenako anakwera wakuda ndipo tsopano akukwera kavalo wotumbuluka. Iye sanabwererenso ndi kukakweranso kavalo woyera. Akavalo onsewa adakalipo, zimangotengera kuti akugwira mu gawo liti ndikuti wakwera kavalo uti. Iye adzakwera kavalo wofiira limodzi la masiku amenewa mu chisautso ndi kupha anthu ambiri. Apa akukwera kavalo wotumbuluka kapena waphulusa. **Kavalo wotumbuluka uyu akuyesera kubweretsa mipingo palimodzi ndi kupanga mpingo umodzi wa dzikolonse. Imeneyo ndiye ntchito yeniyeni ya kavalo wotumbuluka.** Ku Mateyu 24:24, zaikidwa kuti mu masiku otsiriza mizimu iwiri imeneyi idzakhala pafupifupi yofanana moti zidzatengera vumbulutso la Mulungu kuti muone kusiyana. Ndi mzimu umene unali mwa Kaini, Balamu, Yudasi, ndi aneneri onyenga mu m'bado woyamba; ndipo udakali pompano, koma Mulungu watumiza chiombankhanga kuti chitiuze kuti choona ndi chiti.

Chamoyo chachinai chimene mdierekezi anatumiza chinali kavalo wotumbuluka, koma chamoyo chimene Mulungu anatumiza chinali chiombankhanga. Chiombankhanga chimenecho chimatipatsa ife vumbulutso la Mau woona la Mulungu.

Lero zipembedzo zikufuula, kuchita zozwizwitsa, ndikumanena kuti iwo adzazidwa ndi Mzimu Woyera chifukwa akulankhula malilime; koma ife tikudziwa kuti umboni wokhala ndi Mzimu Woyera sikulankhula malilime. Iwo amalankhula malilime ndi kumapempherera odwala, komabe amapitirirabe kuchita misa zawo. Chimenecho ndi chiyani? **Ndi kavalo wotumbuluka, koma chiombankhanga chinabwera, koyamba kudzera mwa M"bale Branham amene anati umboni wa Mzimu Woyera sikulankhula malilime, ngakhale Mzimu Woyera umalankhula malilime. Chiombankhanga chimenecho chabwera ndi kuchotsa chophimba cha mdierekezi ndi kutirora ife kuona chimene satana akuchita.**

Mau akuti dzina la iye amene anakhala pa kavalo ndi Imfa. Kodi imfa ndi chiyani? Imfa ndi kulekana kwathunthu ndi Mulungu. Pamene moyo uchoka mwa china chake, chimafa. Imfa ndi pamene moyo unali. Moyo wachoka mu m'bado uwu wa Laodikaya. Mukudziwa chimene chinabwera? Zokhala mu hade, ziwanda, zinabwera mu mpingo.

Ine sindikukamba za mpingo woona wa Mulungu, koma ine ndikukamba za mu gawo la zipembedzo, World Council of Churches, Mpingo wa chiroma pamodzi ndi mipingo ya chikoka ina. Chivumbulutso 18:2 akuti, *"Wagwa, wagwa, Babulo wankulu, wasandulika mokhalamo ziwanda, ndi mosungiramo mizimu yonse yonyansa."* Ndipo Chivumbulutso 18:4 akuti, *"Turukani m'menemo anthu anga, kuti*

mungayanjane ndi machimo ache, ndi kuti mungalandireko ya miriri yake." Chinthu chimenecho chagwa. Hade anatsatana naye kavalo ameneyu. Ziwanda zimenezo zinasandulika ziwanda zopembedza, koma uthenga wa Mulungu wa chiombankhanga unationetsera ife chimene chiri. Malaki 4:5-6 akukamba za mneneri uyu amene anabweretsanso Mau woona ku mpingo, zimene zinakwaniritsidwa ndi William Branham, wam'thenga wa ku m'bado wa mpingo wachisanu ndi chiwiri. Izi zikuonetsera zisindikizo zoyambirira zinai. "Kavalo woyera" anali wotsutsakhristu mu maonekedwe woyera. "Kavalo wofiira" unali m'bado wophedwa. "Kavalo wakuda" unali M'bado wa M'dima ndi "kavalo wotumbuluka" ndi tsiku limene tikukhalamo tsopano, pamene satana akuyesera kumasula ziwanda zake kuti zilowe ndi kunyenga anthu, koma ife tikuona choonadi chifukwa Mulungu watumiza chiombankhanga. Sipakufunikanso zonena pa za chisindikizo chachinai chifukwa ife tikukhala mu tsiku la kukwaniritsidwa kwake ndipo tikutha kuona chimene chikuchitika mu dziko la chipembedzo ili. Iye anatumiza zamoyo zonse zinai mu dziko kuyang'anira mpando wachifumu wa Mulungu. Mwauzimu, mpando wa chifumu uli mwa anthu ake mu nthawi ino.

Pakutsegulidwa kwa zisindikizo zina zitatu palibe chamoyo choti chilengeze. Izi zikutanthauza chiyani? Zisindikizo zinai zoyambirira izi zikuonetsera m'mene mpingo unagonjetsera mzimu wa wotsutsakhristu kuyambira nthawi imene unayamba mpakana kumapeto. Kotero chisindikizo chachisanu chikuyenera kukhudzana ndi chinachake.

Ine ndikufuna inu mulingalire bwino bwino ndi kukhala ndi chidaliro mu utumiki wamoyo wa nthawi ino. Ife tikupita ku chinachake ku mu chisindikizo chachisanu chimene ndi chosiyana pang'ono ndi zisindikizo zina zinai. Tayang'anani, palibe chamoyo chimene chikulengeza kutseguludwa kwa chisindikizo chachisanu.

Vesi 9: *"Ndipo pamene adamasula chisindikizo chachisanu, ndinaona pansi pa guwa la msembe miyoyo ya iwo adaphedwa chifukwa cha Mau a Mulungu, ndi chifukwa cha umboni umene anali nawo."*

Izi zakhala nthawi zonse zikuganiziridwa kuti miyoyo iyi pansi pa guwa anali akhristu amene anaphedwa chifukwa cha dzina la Ambuye mu M'bado wa M'dima, koma sichoncho. Mulungu watsegula chisindikizo chachisanu ichi. Chikuti, *"Ndinaona pansi pa guwa la msembe miyoyo ya iwo adaphedwa chifukwa cha Mau a Mulungu."* Izi zikanaoneka ngati anali iwo amene anafa mu mibado, okhulupirira mwa Yesu amene anaphedwa. Koma tayang'anani chinthu chimodzi: Iwo anaphedwa chifukwa cha **"Mau a Mulungu ndi umboni umene anali nawo." Palibe pena paliponse pamene pakuonetsera kuti anali ndi "umboni wa Yesu Khristu." Miyoyo pansi pa guwa la msembe ndi Ayuda ophedwa.**

Kuphedwa kwakukulu kwa Ayuda kunachitika pansi pa Hitler kuchokera pafupifupi 1939 mpaka 1945. Kuphedwa kwa Ayuda kunachita pansi pa Hitler, Eichmann, ndi ena otero. Iwo anawapha Ayuda chifukwa chakuti anali Ayuda. Mulungu akufuna Ayuda kuti akhale anthu opatulika. Kotero iwo anapha mamilioni asanu ndi imodzi a iwo Nkhondo ya chiwiri ya dziko lapansi isanafike ngakhale ili nkati chonsecho chifukwa chakuti anali Ayuda; koma iwo anagwiritsitsa Mau a Mulungu. Miyoyo iyi pansi pa guwa ndi Ayuda amene aphedwa chifukwa cha Mau a Mulungu.

Aroma 11:25 akuti, *"kuchita khungu kunadza pang'ono kwa Israeli, kufikira kudzaza kwa anthu amitundu kunalowa."* Mulungu anachititsa khungu Israeli ndipo ngati Mulungu anawachititsa khungu, ndiye zikutanthauza kuti iwo sangathe kumuona Yesu. Chifukwa chiyani Mulungu nachititsa khungu ana ake? Chifukwa chiyani Mulungu anachititsa khungu iwo amene anali ndi lonjezo, ndi iwo amene amasunga lamulo? Kotero kuti Iye akatenge kuchokera kwa Amitundu anthu chifukwa cha dzina lake monga zalembedwera ku chaputala cha khumi ndi chisanu cha bukhu la Machitidwe kumene Yakobo anati, *"Simioni wabwereza kuti poyamba anayang'anira Amitundu, kuti atenge mwa iwo anthu a dzina lake. Ndipo mau a aneneri avomereza pamenepo; monga kunalembedwa, zikatha izo ndidzabwera, ndidzamanganso chihema cha Davide, chimene chinagwa; ndidzamanganso zopasuka zache, ndipo ndidzachiimikanso:"*

Tayang'anani Ayuda awa pansi pa guwa la msembe. **Iwo analibe minjiro.** Ena a oyera mtima amavala bafuta wonyezimira woti mbuu, ndi ena minjiro yoyera, koma Ayuda awa analibe bafuta wonyezimira

woti mbuu, ngakhale minjiro yoyera. Mwa kulankhula kwina, **miyoyo yawo inali yamaliseche pamaso pa Mulungu, koma Mulungu sanawaleke iwo kupita ku Hade; iwo apatsidwa minjiro yoyera.** Ayuda awa anaphedwa chifukwa cha Mau. Mamilioni a iwo anaphedwa chifukwa anali Ayuda ndipo anakhulupirira Mau a Mulungu. Onse a iwo sanapulumutsidwe. Onse amene maina awo anali mu bukhu la moyo anapulumutsidwa. Pali Ayuda ena lero, ndipo analipo nthawi imeneyo, amene samasamala chilichonse cha Mau a Mulungu; iwo sapulumutsidwa, koma Ayuda a chi Orthodox anakhalabe molondora ndi Mau. Iye anakhala moyandikira ndi icho monga anathera, koma Mulungu anachititsa khungu maso ake kumene sanathe kuona Khristu, kuti akathe kutenga mwa Amitundu anthu chifukwa cha Dzina Lake. Miyoyo imene ili pansi pa guwa la msembe ndi Ayuda amene anaphedwa pansi pa Hitler, Eichmann ndi ena otero.

Vesi 10: *"Ndipo anapfuula ndi mau akulu, ndi kunena, kufikira liti, Mfumu yoyera ndi yoona, muleka kuweruza ndi kubwezera chilango chifukwa cha mwazi wathu, pa iwo akukhala pa dziko?"*

Mpingo ukanatha kunena monga, Stefano, kuti akhululukiridwe chifukwa sakudziwa chimene akuchita. Ngakhale Mkwatibwi sakulirira kubwezera kwa mwazi wake; koma Ayuda awa amalira, "Mpakana liti, O Ambuye, woyera ndi woona, muleka kuweruza ndi kubwezera chilango chifukwa cha mwazi wathu iwo akukhala pa dziko?" Iwo mudzawasiya choncho mpaka liti, Ambuye, osawalanga chifukwa cha zimene achita kwa ife? Stefano amene anali gawo la mpingo anati, "Ambuye musawerengere mphulupulu yawo," [akhululukireni.] Umo ndi m'mene mpingo umalankhulira, koma Ayuda awa akulirira kubwezera. Mvetserani chimene chinalankhulidwa kwa iwo.

Vesi 11: *"Ndipo anapatsa yense wa iwo mwinjiro woyera; nanena kwa iwo, kuti apumulebe kanthawi, kufikira atakwaniranso akapolo anzawo, ndi abale awo amene adzaphedwa monganso iwo eni."*

Minjiro yoyera **inaperekedwa** kwa iwo; iwo analibe minjiro yoyera. Iwo sanachite chilichonse pa dziko, monga uthenga wa Yesu ukukhudzidwira, kuti akuyenera minjiro yoyera. **Iwo sanakhulupirire ngakhale mwa Yesu Khristu.** Mulungu anali atawachititsa khungu ndipo iwo anakhala pomwepo ndi lamulo, malamulo khumi, ndi zina. Kotero iwo anali ndi umboni wa Mulungu ndi Mau a Mulungu, ndipo amapfuula pansi pa guwa lamsembe, "Mpakana liti, O Ambuye, woyera ndi woona, muleka kubwezera chilango chifukwa cha mwazi wathu, pa iwo akukhala pa dziko?" Iwo analibe minjiro yoyera koma Baibulo likuti minjiro yoyera inaperekedwa kwa yense wa iwo. Kodi mwinjiro Oyera unali chiyani? Ndi chifundo cha Mulungu. M'malo mowasiya iwo kuti atayike, chifundo cha Mulungu chinali pa iwo. Mulungu anachititsa iwo khungu pa cholinga kuti asaone kuti Khristu anali yani.

Kumbukirani mu masiku a Yosefe m'mene abale ake anamugulitsa iye ku Aigupto, monga m'mene Ayuda anamugulitsira Khristu, koma pamene Yosefe anali ku Aigupto anatenga Mkwatibwi wa Amitundu. Kenako, abale ake anabwera ku Aigupto ndi kupeza chimene Yosefe anali, ndipo iwo anati, "Iye adzatipha ndithu." Ichi ndi chimene Ayuda awa amalingalira atazindikira kuti Khristu anali Messia. Iwo amalingalira kuti Iye akanawapha ndithu, koma monga Yosefe anakhululukira abale ake, kotero Mulungu, mwa Yesu Khristu, Messia, akuwakhululukira Ayuda awa ndikuwapatsa minjiro yoyera. Chifundo cha Mulungu chinawakutira iwo, chifukwa Iye anawachititsa khungu pa cholinga.

Lotsatira la vesi ili likuti, *"Nanena kwa iwo, kuti apumulebe kanthawi, kufikira atakwaniranso akapolo anzawo, ndi abale awo amene adzaphedwa monganso iwo eni."*

Ayuda awa amalirira mwazi wao kuti ubwezeredwe, ndipo anauzidwa kuti ayembekeze mwakanthawi chifukwa abale awo ndi akapolo anzawo amayenera kuphedwa koyamba. Ichi chikutanthauza kuti kuphedwa kukubweranso kwa Ayuda. Iwo adzaphedwanso zikwizikwi, koma Mulungu adzawapatsa iwo amene maina awo ali mu bukhu la moyo minjiro yoyera. Kulingalira kwanu kukhoza kukhala koti, "Kodi iwo akanapulumutsidwa bwanji osalandira Ambuye Yesu Khristu?" Tayang'anani mpingo kudutsa mu M'bado wa M'dima. Oyeramtima samadziwa chilichonse za Ambuye Yesu Khristu. Pamene Kukonzanso kunayamba iwo samadziwa ngakhale kuti umayenera kukhala ndi moyo mwa chikhulupiriro mwa Mulungu. **Iwo amene amakhulupirira Mulungu, mpakana ku mayambiriro a senture uno amakhulupirira kuti Mulungu anali anthu atatu osiyana.** Iwo samazindikira Yesu monga Iye aliri.

Choonadi chinatayika M'bado wa M'dima utayamba ngakhale usanayambe ndipo Yesu amayenera kukhala pamenepo ngati Wamsembe Wankulu kupereka msembe za machimo awo, koma chisomo chake chinalora Amitundu kulowa mu maonekedwe omwewo. Kotero ndi chifukwa chiyani ife tingaganize kuti ndi zachilendo ngati chisomo cha Mulungu chitalora Ayuda kulowa kukhulupirira Mulungu m'modzi, koma osadziwa kuti Yesu anali Messia. Ndi chisomo cha Mulungu kwa Amitundu ndipo ndi chisomo cha Mulungu kwa Ayuda. Inu munganene bwanji kuti Mulungu ndi olakwa powalora Ayuda awa kulowamo. Iye ndi wolondora nthawi zonse. Mulungu ndi wodziimira payekha, ndipo Iye amadziwa kuti akanapanda kuwachititsa khungu iwo akanamulandira Iye. Kotero Iye anawapatsa iwo minjiro yoyera ndikuwauza iwo kuti adikire mpakana abale awo aphedwenso mu chisautso chachikulu.

Pali chinthu chimodzi chofunika kwambiri chimene ine ndikufuna kuti muchione chokhudza chisindikizo chachisanu ichi. **Chili ndi magawo awiri.** Gawo loyamba linachitika pakati pa 1939 ndi 1945. Gawo lachiwiri silichitika mpakana theka lotsiriza la masabata 70 a Danieli.

Komanso, zochitika za chisindikizo chachinai sizinaime pa kuyamba kwa chisindikizo chachisanu, chifukwa chisindikizo chachinai chikuonetsa kavalo wotumbuluka [mzimu wa wotsutsakhristu mu chipembedzo chonama] chidakalipo mpakana kumapeto kwa masabata 70 a Danieli. Koma tithokoze Mulungu, Khristu ndi Mkwatibwi wake ali kunja kwa chisokonekero chachipembedzo chimenecho.

Tsopano pa zokhudzana ndi chisindikizo chachisanu ndi chiwiri, sichinatchulidwepo mu chaputala chachisanu ndi chimodzi; komano sitingafotokoze vumbulutso lochuluka la chisindikizo chachisanu wosaonetsapo kuti chisindikizo chachisanu ndi chiwiri ndi *"mkhalapakati"* pakati pa gawo loyamba ndi gawo lachiwiri la chisindikizo chachisanu, chifukwa gawo loyamba la chisindikizo chachisanu lachitika kale monga ndafotokoza kale. Ife tsopano tikukhala mu *"kanyengo kakang'ono"* ka vesi la khumi ndi chimodzi limene likulekanitsa gawo loyamba ku gawo lachiwiri. M'bado uno, Yesu anati, umene udzaona mtengo wa nkuyu ukuika masamba sudzapita mpaka zinthu izi zonse zitachitika. [Mateyu 24:32-35] Mkuyu kuika masamba mophweka zikutanthauza kusonkhanitsidwa kwa Israeli kubwerera ku dziko la kwawo Ayuda atatha kuphedwa ndi Hitler. Choncho *"kanyengo kochepa"* aka sikadzapitirira m'bado, zimene zikutanthauza kuti uwu ndi m'bado umene udzaone kubwera kwa Ambuye.

Chimene ndikufuna kuti muone ndi chakuti **mkati mwa** *"kanyengo kochepa aka"* zochitika za chisindikizo chachisanu ndi chiwiri zikuchitika ndipo zikumveka bwino mu nyengo iyi, ndipo ife tikukhala mu izo tsopano. Mu *"kanyengo kochepa"* aka wam'thenga wa m'bado wachisanu ndi chiwiri wabweretsa uthenga wake umene unaonetsa mibado isanu ndi iwiri yonse ndi vumbulutso la zisindikizo zonse. Komanso mu *"kanyengo kochepa"* aka utumiki usanu udzabweretsa Mau kufikitsa oyeramtima ku ungwiro. Izi zikuchitika angelo asanu ndi awiri asanaombe malipenga awo ku Israeli.

Pali chinthu chimodzi chinanso chimene ine ndikufuna kubweretsa pazokhudza chisindikizo chachisanu ndi chiwiri. Chisindikizo chachisanu ndi chiwiri chatsegulidwa mu vesi loyamba la Chivumbulutso chaputala chachisanu ndi chiwiri ndi chaputala chachisanu ndi chiwiri chitaikidwa pakati pa kutsegulidwa kwa chachisanu ndi chimodzi ndi chisindikizo chachisanu ndi chiwiri. Chapuatala chachisanu ndi chiwiri cha Chivumbulutso chili ndi zoimirira za bukhu lonse la Chivumbulutso. Chikuonetsa kusindikizidwa kwa 144,000, oyeramtima a mu chisautso, ndipo vesi 15 mpaka 17 likuonetsa ngakhale mzinda, Yerusalemu Watsopano. Inu mudzaziona bwino bwino mu chaputala 21 ndi 22 cha bukhu ili.

Chaputala chachisanu ndi chiwiri chaikidwa pakati pa **chivumbulutso cha zisindikizo chachisanu ndi chamodzi ndi chisindikizo chachisanu ndi chiwiri, koma osati pakati pa pa nthawi ya zisindikizo izi,** kuonetsa kuti bukhu lonse la Chivumbulutso lidzadziwika kwa Mkwatibwi mkwatulo usanachitike. Izi zonse *"zaikidwapakati"* pa gawo loyamba ndi gawo la chiwiri la chisindikizo chachisanu.

Vesi 12: *"Ndipo ndinaona pamene anamasula chisindikizo chachisanu ndi chimodzi, ndipo panali chivomerezi chivomerezi chachikulu, ndi dzuwa linada bii longa chiguduli cha ubweya ndi mwezi wonse unakhala ngati mwazi."*

Vesi 13: *"Ndi nyenyezi za mwamba zinagwa pa dziko, monga mkuyu utaya nkhuyu zache zosapysa pogwedezeka ndi mphepo yolimba."*

Vesi 14*: "Ndipo kumwamba kudachoka monga ngati mpukutu wopindidwa, ndi mapiri onse ndi zisumbu zonse zinatunsidwa kuchoka m'malo mwao."*

Vesi 15: *"Ndipo mafumu a dziko, ndi akuru, ndi akazembe, ndi achuma, ndi amphamvu, ndi akapolo onse, ndi mfulu anabisala ku mapanga ndi m'matanthwe a mapiri."*

Vesi 16*: "Nanena kwa mapiri ndi matanthwe, igwani pa ife, ndipo tibiseni ife ku nkhope ya Iye amene akhala pa mpando wachifumu, ndi ku mkwiyo wa Mwanawankhosa."*

Vesi 17: *"Chifukwa lafika tsiku lalikulu la mkwiyo wao, ndipo akhoza kuima ndani?"*

Chivumbulutso cha chisindikizo chachisanu ndi chimodzi ndichophweka pamene zochitika za mavesi 12 mpaka 17 zikuchitika kamodzi, ndipo izi ndi mu tsiku la Ambuye.

Apa pali chimene chimachitika zochitika za chisindikizo chachisanu ndi chimodzi zisanachitike, zimene zikuchitika mu tsiku la Ambuye. Mngelo woomba lipenga wachisanu ndi chiwiri waomba lipenga lake. Izi ndikuyandikira kumapeto kwa sabata la 70 la Danieli. Kuomba kwa lipenga la chisanu ndi chiwiri kukung'amba chophimba mu kachisi kumwamba mwauzimu. Izi zikubweretsa mpando wa chifumu poyera. Mwakulankhula kwina, zikutsegula Malo Oyeretsetsa, zimene poimirira zikuonetsera kuti palibe chotsalira koma chiweruzo cha Mulungu kuti chitsanulidwe pa mtundu wa anthu ochimwa. Ife tikuonetsa izi mu chaputala cha khumi ndi chimodzi cha bukhu ili.

Tsopano, popewa kubwerezabwereza, ife sitilembanso zomwezi apa. Chimene ine ndikufuna kuti ndionetse apa ndi chakuti malipenga onse akuomba ngakhale limodzi la miriri isanatsanulidwe kumayambiriro kwa mapeto a sabata. Lipenga lachisanu ndi chiwiri, ndipo nthawi yomweyo angelo asanu ndi awiri amene anali ndi malipenga asanu ndi awiri abwera pa mpando wa chifumu kumwamba. Ndiye chimodzi cha zamoyo zinai chikuwapatsa iwo miriri isanu ndi iwiri kuti itsanuledwe kutsiriza mkwiyo wa Mulungu. [Chivumbuluitso 15:6-7]

Angelo asanu ndi m'modzi akutsanula miriri yawo sabata la 70 lisanakwane ndipo nyengo ya chisautso ikutha. Izi zikusiya muriri umodzi, umene ukutsanulidwa pansi pa chisindikizo chachisanu ndi chimodzi mu tsiku la Ambuye, chimene chikuchitika sabata la 70 la Danieli litatha kugwira ntchito. Inde, chisindikizo chachisanu ndi chimodzi ndi muriri wa chisanu ndi chimodzi zikuchitika mu nyengo ya masiku 75 pakati pa kumapeto kwa sabata la 70 la Danieli ndi kumayambiriro kwa ulamuliro wa mileniamu. Nyengo ya masiku 75 imene ndikulankhula apa ikupezeka mu chaputala cha 12 cha Danieli, vesi 11 ndi 12. Nyengo ya masiku 75 imeneyi tikuipeza pochotsera miyezi 42 ku masiku 1260 amene chirombo chikuyenera kulamulira ku [Chivumbulutso 13:5] kuyambira masiku 1335 zimene zikulankhulidwa ku Danieli 12:12. Komanso, kumbukirani kuti nyengo ya miyezi 42 imeneyi apa ndikuyamba ndi kutha kwa msembe za tsiku ndi tsiku pakati pa sabata.

Pali zinthu zina zimene zikuyenera kuchitika kumapeto kwenikweni kwa nyengo ya masiku 75 m'mene Yesu ndi Mkwatibwi wake akubwerera ku dziko lino kukwaniritsa Chivumbulutso 19:11-21 ndi Zakaria 14:3, 5 ndi 12.

Kuukitsidwa kwa oyeramtima a ku chisautso ndi Ayuda amene anafa chifukwa cha Mau a Mulungu kudzachitika mu nthawi iyi, kukwaniritsa Chivumbulutso 11:18 komanso Chivumbulutso 20:4. Komanso, chiweruzo cha mapfuko chikuchitika pamene nyengo iyi ya masiku 75 ikutha. Izi zalembedwa ku Mateyu 25:31-46.

Ine ndimangofuna ndinene apa chiukitsiro ndi chiweruzo cha mapfuko, chifukwa chikuchitika pamene chisindikizo chachisanu ndi chimodzi chikukwaniritsidwa kwathunthu mu tsiku la Ambuye.

Tsiku lalikulu la Ambuye ili likuchitika nthawi yomweyo nyengo ya chisautso ikangotha monga Mateyu 24:29-30 akunenera, *"Koma pomwepo, atapita masauko a masiku awo, dzuwa lidzadetsedwa, ndi mwezi sudzaonetsa kuwala kwache, ndi nyenyezi zidzagwa kuchokera kumwamba, ndi mphamvu za kumwamba zidzagwedezeka. Ndipo pomwepo padzaoneka m'thambo chizindikiro cha mwana wa munthu,*

ndipo mitundu yonse ya pa dziko lapansi idzadziguguda pa chifuwa, nidzapenya Mwana wa munthu alinkudza pa mitambo ya kumwamba, ndi mphamvu ndi ulemerero waukulu." Potsiriza kuwerenga malemba awa, wina akhoza kutseka maso ake auzimu kuti asaone chisindikizo chachisanu ndi chimodzi ichi.

Ndiloreni ndilankhule potseka chaputala ichi, palibe chilichonse pa chisindikizo chachisanu ndi chiwiri, bata lokha, panalibe choti chilankhulidwe. Tachionani ichi pamene bukhu laling'ono ili likufutukuka ndi zomatira mozungulira ilo. Mwana wankhosa anachotsa chomatira choyamba ndipo kuseri kwake kunalembedwa kavalo woyera, kuseri kwa chachiwiri kunali kavalo wofiira, kuseri kwa chachitatu kunali kavalo wakuda, kuseri kwa chachinai kunali kavalo wotumbuluka; kuseri kwa chachisanu, miyoyo imene ili pansi pa guwa, ndipo kuseri kwa chachisanu ndi chimodzi, tsiku la Ambuye. Chinachake chinalankhulidwa pamene chisindikizo chilichonse chimatsegulidwa koma bukhulo silinatsegulidwe. Bukhulo silikanatsegulidwa pansi pa choyamba, chachiwiri, chachitatu, chachinai, chachisanu, kapena chachisanu ndi chimodzi, **koma pamene chachisanu ndi chiwiri chikutsegulidwa chifukwa chiyani pamafunika chinachake chilankhulidwe?** Pali bata. Bukhu lonse likanatsegulidwa, kutanthauza kuti ulamuliro wa Yesu Khristu waikidwanso mwa Mkwatibwi. Amen.

CHIVUMBULUTSO CHAPUTALA CHACHISANU NDI CHIWIRI

Tisanalowe mu chaputala chachisanu ndi chiwiri, ndikufuna ndifotokoze kwa inu kuti pali sabata limodzi, kapena nyengo ya zaka zisanu ndi ziwiri, yotsalira ku pfuko la Israeli. Nyengo ya zaka zisanu ndi ziwiri imeneyi ikutchedwa "Sabata la 70 la Danieli." Ndi nyengo ya zaka zisanu ndi ziwiri imene Mulungu akuchita ndi Israeli nthawi ya Amitundu itatha. Palibe imodzi ya iwo imene yakwaniritsidwa kale. Chaputala cha chisanu ndi chiwiri ichi chikuyamba zaka zotsiriza izi ku Israeli, ndicho chifukwa chake ife tikubweretsa sabata la 70 kumayambiriro kwa chaputala ichi.

Tiyeni titsegule ku bukhu la Danieli ku malemba ena. Izi zitithandiza kuti timvetse bwino bukhu la Chivumbulutso. Danieli anali ku Babeloni ndipo amafuna kudziwa ndi nthawi yochuluka bwanji anali nayo komanso ndi liti adzaomboledwe.

Danieli 9:20-21 akuti, *"Pakuti pakunena ine ndikupemphera, ndikuvomereza tchimo langa, ndi tchimo la anthu a mtundu wanga Israeli, ndi kutula chipembedzero changa pamaso pa Yehova Mulungu wanga, chifukwa cha phiri lopatulika la Mulungu wanga, inde pakunena ine m'kupemphera, munthu uja Gabrieli, amene ndidamuona m'masomphenya poyamba paja, anauluka mwa liwiro nandikhudza ine ngati nthawi yakupereka msembe ya madzulo." "Nthawi yakumadzulo"* iyi ndi msembe yakumadzulo imene a Israeli adzaperekanso mu tsiku ili lotsiriza ndipo wotsutsakhristu adzapangitsa iwo kuima pakati pa sabata.

Danieli 9:22 akuti, *"Ndipo anandilangiza ine ndikulankhula nane, nati, Danieli iwe, ndatuluka tsopano ine kukuzindikiritsa mwa luntha."* Tayang'anani mzimu wotumikira umenewo ukubwera kwa Danieli. Mzimu wotumikira umenewo unabwera kwa iye kudzamupatsa iye luntha ndi kumvetsa pa Mau a Mulungu. Mu tsiku ili lotsiriza Mulungu adzakhala ndi utumiki utadzuka kuti ufikitse ku ungwiro oyeramtima ake amene angatenge Mau ndikuwagwira iwo ndi luntha ndi kumvetsa. Ndiye pamene zisindikizidwa ndipo inu ndikuwerenga ndi kumvetsa, ndiye inunso mukhoza kukhala ndi luntha ndi kumvetsa mu Mau a Mulungu.

Danieli 9:23 akuti *"Pakuyamba iwe mapembedzero ako, linatuluka lamulo, ndipo ndadza ine kukufotokozera, pakuti ukondedwa kwambiri, zindikira tsono mau awa, nulingirire masomphenyawo."* Danieli anakondedwa kwambiri ndi Mulungu, kotero Mulungu anamuonetsa iye chimene chidzachitike kwa anthu ake. Mosakaika, Danieli samamverera kuti anali wokondedwa wa Mulungu chifukwa iye amavomereza machimo ake ndi machimo a anthu ake. Iye kwenikweni amamverera kuchepa kumeneko

ku Babeloni, koma mngelo anabwera ndikunena kuti, “Danieli, Mulungu amakukonda iwe, ndipo iye akufuna kukuuza chinachake.”

Taonani vesi lotsatira, Mulungu adamulora Danieli kudziwa zokhudza “nthawi.” Zisanu ndi ziwiri zikutanthauza “sabata” ndipo apa pali “masabata a zaka.” Choncho “masabata makumi asanu ndi awiri” zikutanthauza kuti kunali zaka 490 zotsalira ku Israeli. Umu ndi m’mene zikukhalira.

Danieli 9:24-26 akuti *“Masabata makumi asanu ndi awiri alamulidwa anthu a mtundu wako dni mudzi wako, wopatulika kumariza cholakwacho, ndi kutsiriza machismo, ndi kutetezera mphulupulu, ndi kufikitsa chilungamo chosalekeza, ndi kukhomera chizindikiro masomphenya ndi zonenera, ndi kudzoza malo opatulikitsa.*[Pali masabata 70 zimene ndi zaka 490 ku Israeli kuyambira nthawi imene analandira lamulo pamene iwo anali ku Babeloni.] *Dziwa tsono, nuzindikire, kuti kuyambira kutuluka lamulo la* ***kukonzanso, ndi kum’manga Yerusalemu,*** *kufikira wodzozedwayo, ndiye kalonga, kudzakhala masabata asanu ndi awiri, ndi masabata makumi asanu ndi limodzi mphambu awiri makwalala ndi chemba zidzamangidwanso, koma mu nthawi za mavuto.* [Vesi 25 ikulankhula za kumangidwa kwa **mzinda** Khristu asanafike nthawi yoyamba.] *Ndipo atapita masabata makumi asanu ndi limodzi mphambu awiri wodzozedwayo adzalikhidwa, nadzakhala opanda kanthu, ndi anthu a kalonga wakudzayo adzaononga mudzi ndi malo opatulika, ndi kutsiriza kwake kudzakhala kutsiriza kwa chigumula, ndi kufikira chimaliziro kudzakhala nkhondo, chipasuko chalembedweratu.”* **Panali masabata asanu ndi awiri ndi masabata 62 zimene zikupanga masabata 69. Ayuda anali ndi masabata 70 okha oikidwa kwa iwo ndi masabata 69 anali atadzaza mpakana mu nthawi imene Messiah anaphedwa. Choncho ngati masaba 69 akwaniritsidwa ndi nthawi yochuluka bwanji imene Ayuda atsala nayo. Sabata linanso limodzi. Ndipo sabata imeneyo ndi zaka zisanu ndiziwiri zina zotsalira mileniamu isanayambe.**

Apa akuti anthu akaronga adzabwera ndi kuononga mzinda ndi malo opatulika. Ndani amene adaononga mzinda ndi malo opatulika mu 70A.D.? Anali Aroma. Apa akuti “ndipo anthu akaronga adzabwera,” karonga walembedwa ndi; “k” wang’ono kuonetsera kuti iye ndi karonga wabodza, wotsutsakhristu. Izi zikuonetsera kuti wotsutsakhristu adzachokera ku Roma. Taonani mmene ndi kulankhulira izi; *“anthu a karonga adzabwera.”* Anthu a karonga anali Aroma mu 70A.D, komano karonga adzabwera pafupifupi zaka 2000 zitatha ndi kukhala mu kachisi m’menemo mu Yerusaremu? **Iye ndi amene adzaphwanya pangano ndikupangitsa msembe kutha. Ameneyo ndi papa mu nthawi yotsiriza!**

Palibe pena paliponse mu Baibulo pamene akuti Yesu anaphedwa pakati pa sabata. Ndibwereza kuti zimveke. **Palibe malo ena aliwonse mu Baibulo pamene akuti Yesu anaphedwa pakati pa sabata.** Iye anaphedwa patatha masabata 69, ndipo apo pakutsarira sabata lina limodzi zaka zina zisanu ndi ziwiri, ku pfuko la Israeli. Karonga amene akupanga pangano ndi papa.

Tiyeni tiwerenge Danieli 9:27.izi zikukamba za karonga; wotsutsakhristu; kapena papa. *“Ndipo iye adzapangana chipangano cholimba ndi ambiri sabata limodzi; ndi pakati pa sabata adzalekanitsa nsembe ndi msembe ya ufa ndi pa phiko la zonyansa padzafika wina wakupasula, kufikira chimaliziro cholembedweratu, mkwiyo udzatsanulidwa pa wopasulayo.”* Iye adzapanga pangano kwa sabata limodzi, zaka zisanu ndi ziwiri.

Kodi sabata la 70 lidzayamba liti? Mulungu ndi amene akupangitsa sabata. Sikuti papa adzayamba ntchito ndi kuisiya kwa zaka zisanu ndi ziwiri; koma Mulungu ndi amene akuyamba nthawi. Mulungu adzayamba sabata la 70 la Danieli mwa zinthu zimene iye akuchita. Ndi Mulungu amene amachita zimenezo.

Papa adzapanga pangano ndi Israeli komanso mapfuko ena ambiri. Ayuda adzayambanso kupereka msembe pamene kachisi akumangidwanso; koma pakati pa sabata papa adzaswa pangano lake la kwa Ayuda ndi kupangitsa msembe kuima. Iye adzawauza Ayuda kuti asaperekenso msembe. Izi zikuchitika pakati pasabata. Iye adzachita chiyani tsopano? Papa adzasuntha ofesi yake ndi kuika mukachisi amene adzamangidwa malo omwewo akachisi wa Solomo. [2 Atesalonika 2:3-4.]

Tsopano pofotokozanso chaputala cha chisanu ndi chiwiri cha bukhu la Chivumbulutso. Itatha mibado isanu ndi iwiri ya mpingo, Yohane akutengedwa mu Mzimu. Iye ali mu masomphenya, gawo lina la nthawi iye ali kumwamba ndipo gawo lina ali padziko mu masomphenya awa akuona zinthu zina zikuchitika. Mu chaputala chachinai ndi chaputala chachisanu iye anali kumwamba. Mu chaputala chachisanu ndi gawo lina la chaputala chachisanu ndi chimodzi Yohane akuona chinachake chikuchitika pa dziko. Apa mu chaputala cha chisanu ndi chiwiri iye akuona chinachake chikuchitika mudera ya maonekedwe. Iye akulidziwa dera limenelo chifukwa ndi kum'mawa chapakati, pa mtima pa dziko. Yohane akuyamba kuona china chake chikuchitika.

Chivumbulutso, chaputala chachisanu ndi chiwiri vesi 1: *"Zitatha izi ndinaona angelo anai ali nkuimirira pa ngodya zinai za dziko, kuti ingaombe mphepo pa dziko, kapena pa nyanja kapena pa mtengo uli wonse."*

Ife tikudziwa kuti dziko ndi lozungulira. Pamene tiona angelo awa akuima pa ngodya zinai za dziko, zikuoneka ngati dziko liri ndi makona anai ndi mngelo woimirira pakona liri lonse kugwira mphepo zinai. Koma siziri choncho, Yohane adawaona angelo anai awa akuima Kum'mawa Chapakati.

Ku United States wa Amerika tili ndi chimene chikutchedwa ngodya zinai za ma state. Ndi pamene New Mexico, Arizona, Utah, ndi Colorado amakumana. Inu mukhoza kuika mwendo umodzi mu Arizona, ndi wina mu Utah, ndi dzanja limodzi mu New Mexico ndi lina mu Colorado. Awa ndi malo okhawo mu United States wa America kumene inu mukhoza kuchita izi. Inu mukhoza kukhala mu ma state anai nthawi imodzi. Ndi pamene ma state anai amakumana.

Ndimalankhula izo kuti ndinene izi. Apa, pamene angelo anai akuimirira pa ngodya zinai za dziko, zikutanthauza kuti akuima pamene mbali ili yonse ikuyambira, kum'mawa, kumadzulo, kumpoto ndi kumwera. Ndi kumene kum'mawa kukumana ndi kumadzulo ndi kumpoto kukukumana ndi kumwera, kum'mawa kwenikweni. Ndi kumene nthawi inayambira, ndi kumene nthawi idzathera.

Angelo anai awa akuimirira pa ngodya zinai za dziko kugwira mphepo zinai kuti zisaononge dziko ndi kuyamba nkhondo yaikulu ya Armagedoni.

Tikhoza kungonena kuti mphepo zinai zimenezi zikuonetsera nyengo za dziko zinai. Izo zakhala zili. Inu mukhoza kuziika ngati mphamvu za chipembedzo, mphamvu za nkhondo, mphamvu za chuma, ndi mphamvu za ndale. Izi ndi mphepo zinai zimene angelo awa akugwira kutetezera dziko mpakana Mulungu atasindikiza Ayuda 144,000.

Vesi 2: *"Ndipo ndinaona mngelo wina, anakwera kuchokera potuluka dzuwa, ali nacho chizindikiro cha Mulungu wamoyo, ndipo anapfuula ndi mau akulu kuitana angelo anai, amene adalandira mphamvu kuipsa dziko ndi nyanja."* Vesi 3: *"Nanena, musaipse dziko, kapena nyanja, kapena mitengo, kufikira tidasindikiza chizindikiro akapolo a Mulungu wathu, pa mphumi pao."* Ngati dziko ili lozungulira ndipo mukachoka ku Yerusalemu ndikupita chakumadzulo ndikumapitirira, ndiye inu mudzafika ku Yerusalemu kuchokera ku mmawa. Ndinjira imene mngelo wayendera kudutsa mu nthawi ndi uthenga, kuchokera ku Yerusalemu anapita kumpoto, mpakana wapita kuzungulira dziko ndi Uthenga. Ndicho chifukwa iye akukwera kuchokera ku m'mawa kubweretsa uthenga ku Yerusalemu.

Angelo anai akugwira mphepo zinai, ndipo mmene Yohane amazionera, zimakhala ngati iwo amafuna kulora mphepo zimenezi kuononga dziko ndi kufikitsa dziko ku mavuto ku Armagedoni. Koma Mulungu akuti osalora mphepo ziombe; kuti sinthawi yoti ziombe. Pakuyenera kukhala nthawi imene Uthenga ukuyenera kulalikidwa ku Israeli.

Mngelo m'modzi amaulukira mwamba ndipo iye amati osaononga nyanja kapena mtunda, koma kuti agwiritse nyengo za dziko izi. Chifukwa chiyani? Gwirani nyengo ya dziko kufikira "ife"aneneri awiri aku Chivumbulutso chaputala 11, titasindikiza 144,000 a ana a Israeli. **Pamene mngelo wa nthawi akubweretsa uthenga ku Yerusalemu, nthawi ya Amitundu idzakwaniritsidwa.** Zochitika zazikulu za Uthenga zidzachitika muYerusalemu

Pamene mngelo anaulukira ku Germany, zochitika zazikulu za Uthenga zinali ku Germany. Pamene mngelo anaulukira ku England, zochitika zazikulu za Uthenga zinali ku England. Mngelo ndi uthenga,

mngelo ndi chisindikizo cha Mulungu Wamoyo wauluka kale kudutsa kupyola mu United State wa Amerika. Amerika sadzagwedezeka pansi pa mphamvu ya chitsitsimutso monga anachitira nthawi ina. Chimene chatsalira ndi ungwiro wa oyera mtima, khristu akupangidwa mwa Mkwatidwi ndipo Mau kukumangani mwa Yesu Khristu. Masiku a zitsitsimutso zogwedeza dziko atha tikanena za mpingo wa dziko kulandira chilichonse.

Panalibenso nthawi inayake masiku a Martin Lutera atatha pamene Germany anakhalanso ndi chitsitsimutso. Atatha masiku a Yohane Wesile sipanakhalenso nthawi imene Mulungu anayendera England mu chitsitsimutso chogwedeza pfuko. **Mneneri komanso wam'thenga wa Mulungu mu nthawi ino, William Branham, analosera mu 1957 mu mzinda wa Chicago kuti chinali chaka chimene Amerika akanalandira uthenga kapena kuukana, ndipo kuyambira 1957 iye wakhala mopendekeka. Iye wakhala akutsika ndipo sadzakweranso muchitsitsimutso china. Pfuko ili latha, pokamba za "chitsitsimutso chogwedeza dziko," sichidzachitikanso.**

Inu mukuganiza kuti azimai akuvala moipa, azibambo akuchita moipa, ndipo mumizinda simuli motetezeka kwa anthu akale kukhala mu park; tchimo lakula mu dziko ndipo zidzakhala moipa ndi moipa pamene chiwanda chilichonsechikumasulidwa ndikubwera poyera. Pamene zotsalira za uthenga zikusiya dziko, ziwanda zimabwera ndikutsogolera. Malo otsalira amene Uthenga udzakhala ndi chochita ndi mumzinda wa Yerusalemu.

Baibulo likuti ku Aroma 11:25 kuti *"kuuma mtima kunadza pang'ono pa Israeli, kufikira kudzadza kwa anthu Amitundu kunalowa"* [kapena mpakana nthawi ya amitundu itatha.]

Pamene Mulungu ayamba kukwaniritsa chaputala chachisanu ndi chiwiri cha Chivumbulutso, masiku a Amitundu atha. Pamene Israeli anakhala pfuko zimaonetsera kuti kutha kwa m'bado wa Amitundu kunali pafupi, osati kuti unatha tsiku lomwelo, koma Baibulolikuti m'bado uwu sudzapita mpakana zinthu zonse izi zitakwaniritsidwa.

Pamene Hitler, Eichmann, ndi ena anapha Ayuda 6million, zanenedwa kuti awa akuyenera kuyembekeza kanthawi pang'ono mpakana akapolo anzawo aphedwenso monga iwo. Nthawi pang'ono imeneyo siidzapitirira m'bado, chifukwa m'bado umene ukuona Israeli akubwerera kwao sudzapita mpakana Ambuye abwera, mpakana zonse zitakwaniritsidwa.

Yohane anayang'ana ndi kuona angelo akukwera kuchokera ku m'mawa ndi chisindikizo cha Mulungu wa moyo, ndi uthenga wa Israeli. [Tayang'anani amene iye akuwasindikiza.] Mngelo uyu akubwera ndi kulankhula osaononga dziko, nyanja, kapena mitengo mpakana titasindikiza akapolo a Mulungu wathu pa nthumi pawo. Sikuti ali ndi chidindo ndipo akuwadinda iwo pa mphumi, koma pansi pa uthenga wa aneneri awiri aku Chivumbulutso 11; iwo adzatenga vumbulutso mu lingaliro lawo la uzimu la chimene Yesu ali.

Vesi 4: *"Ndipo ndinamva chiwerengero cha iwo osindikizidwa chizindikiro, zikwi makumi khumi ndi makumi anai, osindikizidwa chizindikiro mwa mafuko onse a ana aIsraeli."*

Kodi mukuona chimene chili? Ndi Uthenga kupita ku Israeli. Zilibe chochita ndi Amitundu, amene athana nawo. Inu mutati mutsegule maso anu auzimu ndikuyang'ana lero mukanatha kuona kuti zatha tsopano. Apa pakubwera aneneri awiri akusindikiza 144,000…, 12,000 kuchokera ku pfuko lili lonse

Vesi 5: *"Mwa pfuko laYuda anasindikizidwa chizindikiro zikwi khumi ndi ziwiri. Mwa pfuko la Rubeni zikwi khumi ndi ziwiri. Mwa pfuko la Gadi zikwi khumi ndi ziwiri."*

Vesi 6*: "Mwa pfuko la Aseri zikwi khumi ndi ziwiri. Mwa pfuko la Nafitali zikwi khumi ndi ziwiri. Mwapfuko la Manase zikwi khumi ndi ziwiri"*

Vesi 7*: "Mwa pfuko la Simioni zikwi khumi ndi ziwiri. Mwa pfuko la Levi zikwi khumi ndi ziwiri. Mwa pfuko la Isakara zikwi khumi ndi ziwiri."*

Vesi 8: *"Mwa pfuko la Zebuloni zikwi khumi ndi ziwiri. Mwa pfuko la Yosefe zikwi khumi ndi ziwiri. Mwa pfuko la Benjamini anasindikizidwa chizindikiro zikwi khumi ndi ziwiri."*

Panali 144,000 amene anasindikizidwa mwa mapfuko khumi ndi awiri a Israeli. Iwo anali kuti? Iwo anasonkhananso ku dziko la kwao. Ndi chifukwa chake Mulungu anamasula Hilter ndi kumulora iye kudana ndi Ayuda. Iye anawathamangitsira iwo ku dziko la kwao kuti akakhale nawo kumeneko, chifukwa mngelo uyu anachokera cha ku madzulo kwa nyanja ku USA, kubwerera ku Yerusalemu, ndipo 144,000 awa amayenera kukhala mu Israeli pamene mngelo uyu amene ali ndi Uthenga afika kusindikiza iwo ndi chisindikizo cha Mulungu pamene avomereza Khristu.

Ndi liti adzasindikizidwe 144,000 awa? Iwo akusindikizidwa mu chigawo choyamba cha sabata la 70 la Danieli, chifukwa iwo akupita kuchenjeza dziko la pansi mu gawo lachiwiri la sabata limenelo kuti asalambire kachitidwe ka chibabulo. Pamene iwo alandira chisindikizo chawo, iwo akupita ku pfuko lili lonsekumene anachokera ndi kuchenjeza dziko, ndipo iwo akulalikira uthenga wosatha monga zalembedwa ku Chivumbulutso 14 ndi 18.

144,000 awa asindikizidwa mwa uthenga wa aneneri awiri, amene ndi amuna awiri okhala ndi mzimu wa Mose ndi Eliya, ndipo iwo adzaima pamenepo mu misewu ya ku Yerusalemu kumanenera.

Tsopano Yohane akuwona chiwerengero china. Iye anawadziwa 144,000 kuti anali ndani, chifukwa anali muyuda iye mwini. Iye sanafunse za iwo. Iye analibe zambiri zolankhula za iwo. Kenako anaona khamu lina lalikulu mu vesi 9.

Vesi 9: *"Zitatha izi ndinapenya, taonani, khamu lalikulu, loti panalibe munthu anankhoza kuwerenga, ochokera mwa mtundu uli wonse ndi mafuko ndi anthu ndi manenedwe, akuimirira ku mpando wachifumu ndi pamaso pa Mwana wankhosa, atabvala zovala zoyera, ndi makhwatha akanjedza m'manja mwao."*

Taonani kuti masomphenya a Yohane akubwerera mu gawo la mwamba mwamba ndipo iye akuona chiwerengero chachikulu pa mpando wa chifumu. Taonani zimene iwo avala, chifukwa ndi zofunika. Kodi iwo ali ndi bafuta woti mbuu woyera, monga Mkwatibwi? Ayi. Iwo ali ndi mwinjiro woyera, chovala choyera chawamba, koma Mkwatibwi wa Yesu Khristu wavala bafuta woti mbuu chimene ndi chilungamo chake cha Mulungu. [Chivumbulutso 19:7-8] Choncho, awa si Mkwatibwi koma oyeramtima a ku chisautso.

Khamu lalikulu limeneli limene linali pa mpando wa chifumu si ena ai koma anamwali opusa a ku Mateyu 25, ndi oyera mtima a Mulungu amene adakali ku Babulo pakati pa sabata la 70 la Danieli pamene papa aphwanya pangano lake ndipo chisautso chachikulu chikuyamba ndipo iwo akuitanidwa ndi alaliki 144,000 achiyuda.

Tiyeni tsopano tilekanitse anamwali opusa ku "amene akugonabe" oyeramtima akuzipembedzo motalika kuti tiwapatse chizindikiro, ndipo kenako kuwaikanso pa mpando wachifumu ngati gulu limodzi, monga oyeramtima a muchisautso.

Tiyamba kuchita ndi anamwali opusa a ku Mateyu 25 amene akubwera kugogoda chitseko chitatsekeka, popanda Mau a mu nthawi ino iwo sangapite mu Mkwatulo. Ndiye kenako iwo akuyamba kutenga Mau, ndipo pamene iwo ali mu njira kuyesera kutenga Mau, [Mateyu 25:10] Mkwatulo ukuchitika ndipo iwo akutsala pano pa dziko.[Nthawi yomweyo, pamene izi zikuchitika, *akhristu aku zipembedzo* akadali kugona mu mipingo yawo ya chipembedzo, koma iwo adzatuluka pansi pa uthenga wa 144,000 mu gawo lotsiriza la zaka zitatu ndi theka la sabata la 70 la Danieli.] Koma anamwali opusa awa adzadzuka kumayambiriro kwa sabata la 70 la Danieli za chisoni kuti mkwatulo umene amauyembekezera wachitika kale, ndipo iwo atsala pa dziko. [Mateyu 25:11]

Mosakaika anamwali opusa awa apa Mateyu 25 adzakhala mboni motsutsana ndi kachitidwe kabodza ka mpingo ka dziko lapansi mugawo loyamba la sabata la 70 la Danieli; pamene aneneri awiri akuonekera ku Israeli kutulutsa Ayuda 144:000 kuti akhale mboni motsutsana ndi Babulo mu zaka zitatu ndi theka zotsiriza za sabata. Anamwali opusa ali gawo la khamu lalikulu limene linaima pa mpando wa chifumu wa Mulungu. Ngakhalenso akhristu akuzipembedzo amene adzagwedezedwa ndi 144,000 kuchoka mu zipembedzo mugawo lotsiriza la zaka zitatu ndi theka zotsiriza za sabata ndipo palimodzi adzapanga akhristu akuchisautso amene anaima pa mpando wa chifumu ndipo oyera mtima amu nyengo zina adzaimiriridwanso. Mulungu yekha ndi amene akudziwa chiwerengero chonse apa. Uthenga umene

144,000 akulalikira ukufotokozera mu chaputala cha khumi ndi chinai ndicha khumi ndi chisanu ndi chitatu cha bukhu ili.

Komanso ophedwa palimodzi ndi oyeramtima a kuchisautso awa adzakhala Ayuda ambiri amene sakumudziwa Yesu Khristu, koma iwo akuima ndi Mau amene anaperekedwa kwa iwo mu chipanganochakale ndi Mose. Wotsutsa akupha Ayuda awa chifukwa cha **Mau a Mulungu,** osati umboni wa Yesu. Awa onse adzapatsidwa minjiro yoyera. Palimodzi, oyeramtima ndi Ayuda ophedwa ataima panyanja ya mandala mu chaputala 15 cha bukhu ili.

Vesi 10: *"Ndipo anapfuula ndi mau akulu, nanena, chipulumutso kwa Mulungu wathu wakukhala pa mpando wachifumu, ndi kwa Mwanawankhosa."*

Vesi 11: *"Ndipo angelo onse anaimirira pozinga mpamdo wachifumu, ndi akulu, ndi zamoyozo zinai, ndipo anagwa nkhope yao pansi ku mpando wa chifumu, nalambira Mulungu."*

Vesi 12: *"Ndi kunena, Amen: Thambo ndi ulemelero, ndi mzeru, ndi chiyamiko, ndi ulemu, ndi chilimbiko, ndi mphamvu zikhale kwa Mulungu wathu kufikira nthawi za nthawi. Amen."*

Vesi 10: ikuonetsa oyeramtima awa akupereka ulemelero kwa Mulungu chifukwa cha chipulumutso chawo pamene iwo anapfuula kuyamika Mulungu ndi mau amodzi.

Mavesi 11 ndi 12, akuonetsa zonse kumwamba kupembedza Mulungu pamene khamu lalikulu ili mu vesi lachisanu ndichinai linaima pa mpando wa chifumu woomboledwa. Iwo anali atapereka miyoyo yawo chifukwa cha Mau, ndipo tsopano anali kumwamba atavala mwinjiro yoyera. Angelo, akulu, ndi zamoyo zinai zinagwa nkhope zawo ndi kupembedza Mulungu pamene anaona khamu lalikulu limene linapulumutsidwa.

Pamene Yohane anali ataima pamenepo ndikumayang'ana izi kumwamba, m'modzi mwa akulu anayamba kumufotokozera Yohane chimene zimatanthauza, monga m'mene ine ndafotokozera kwa inu, owerenga.

Vesi 13: *"Ndipo m'modzi wa akulu anayankha, nanena ndi ine. Iwo abvala zovala zoyera ndiwo ayani, ndipo achokera kuti?"*

Vesi 14 *"Ndipo ndinati kwa iye, Mbuye wanga, mudziwa ndinu. Ndipo anati kwa ine, iwo ndiwo akutuluka muchisautso chachikulu, ndipo anatsuka zovala zao, naziyeretsa m'mwazi wa Mwanawankhosa."*

Iwo anatuluka mu chisautso chachikulu, ndipo amayenera kuyeretsa minjiro yawo.**Iwa ndi iwo amene anaima pa nyanja yamandala imene ikuyaka ndimoto muchaputala chakhumi ndi chisanu cha Chivumbulutso.** Iwo anabwera mu nyengo ya chisautso chifukwa iwo sanathe kumvera atumwi a Mulungu, aneneri, alaliki, abusa ndi aphunzitsi amene anadzuka kufikitsa Mkwatibwi ku ungwiro. Mau adzafikitsa ku ungwiro anthu ambiri ndipo iwo amene safika ku ungwiro adzalowa mu chisautso. Palibe malo ena aliwonse a iwo. Iwo akuyenera kudzapereka miyoyo yawo chifukwa cha Uthenga wa Yesu Khristu mu
nyengo yaikulu imeneyo ya chisautso. Ine ndikukamba za iwo amene abadwa mwatsopano, koma kulephera kupita mu Mkwatulo.

Vesi 15: *"Chifukwa chache ali ku mpando wa chifumu wa Mulungu, ndipo amtumikira iye usana ndi usiku m'kachisi mwache, ndipo Iye wakukhala pa mpando wachifumu adzawachitira mthunzi.*"

Vesi 16: *"Sadzamvanso njala, kapena ludzu, kapena silidzawatentha dzuwa, kapena chitungu chili chonse."*

Vesi 17*; "Chifukwa Mwanawankhosa wakukhala pakati pa mpando wachifumu adzawaweta, nawadzawatsogolera ku akasupe amadzi amoyo, ndipo Mulungu adzawapukutira misozi yonse pamaso pawo."*

Kodi zikutanthauza chiyani pamene akuti *"sadzamvanso njala?"*Iwo anali ndi njala. Iwo sakanatha kugula kapena kugulitsa chifukwa anakana chilemba cha chirombo. Iwo anaona vumbulutso la izo mochedwa. Iwo anaona chimene chirombo chinali Mkwatulo utachitika. Kotero, iwo sakanatha kutenga

chilembo cha chirombo ndipo, mosakaika iwo amayenera kukhala ndi njala. Ambiri a iwo amavutika mpaka imfa, chifukwa sangatenge chilembo cha chirombo kapena kupembedza fano lake.

Vesi 15, 16, ndi 17 ikuonetseranso **oyeramtima akuchisautso adzakhala gawo la mzinda wa Mulungu pamene kumwamba kwa tsopano ndi dziko latsopano libwera.** Izi zafotokozedwa mu chaputala 21 ndi 22.Amen

CHIVUMBULUTSO CHAPUTALA CHACHISANU NDI CHITATU

Vesi1: *"Ndipo pamene anamasula chisindikizo chachisanu ndi chiwiri, munali chete m'Mwamba monga mwa nthawi ya ora latheka."* Vesi loyamba la chaputala ichi likuchita ndi kutsegulidwa kwa chisindikizo chachisanu ndi chiwiri. Pamene tikuphunzira zisindikizo tikupeza kuti nthawi iliyonse chisindikizo chimatsegulidwa china chake chimalanthulidwa kapena chinachake chimalembedwa, koma pamene chisindikizo chachisanu ndi chiwiri chikutsegulidwa palibe chilichonse cholembedwa kapena chilichonse chonenedwa. Chifukwa chiyani? Chifukwa bukhu lonse latsegulidwa, ndipo Mngelo Wamkulu ameneyo akubwera ku Chivumbulutso, chaputala 10 ndi bukhu lotsegulidwa mu dzanja Lake. Ife tipeza zambiri za vesi ili mu chaputala cha khumi.

Lipenga limodzi lisanalire, mibado isanu ndi iwiri ya mpingo, zisindikizo zisanu ndiziwiri, mabingu asanu ndi awiri, amene ndi mavumbulutso a zisindikizo zisanu ndi ziwiri adziwika ku mpingo, chifukwa, apa, angelo asanu ndi awiri abweranso pa mpando wachifumu.

Vesi 2: *"Ndipo ndinaona angelo asanu ndi awiri amene amaimirira pamaso pa Mulungu, ndipo anawapatsa malipenga asanu ndi awiri."*

Kodi mukuona kusintha uku? Kwa iwo kunapatsidwa malipenga asanu ndi awiri. Iyi nthawi ya kusintha. Iwo achita kale ntchito zina, ndipo pano akupatsidwa malipenga asanu ndi awiri kuti aombe, ndipo pamene akuomba padzakhala china chake chikuchitika padziko. **Awa ndi angelo womwewo asanu ndi awiri amene anali ndi mibado ya mpingo, zisindikizo, ndipo iwo ndi mabingu asanu ndi awiri amene analankhula mawu awo kupyolera mwa mau a wam'thenga wa chisanu ndi chiwiri wa m'bado wa mpingo kudzadziwitsa vumbulutso la zisindikizo zisanu ndi ziwiri.** Ichi ndi chifukwa chake mibado ya mpingo, zisindikizo, mabingu zidzachitika ngakhale lipenga limodzi lisanaombe. **Ndi angelo omwewo asanu ndi awiri auzimu.** Iwo alinso ndi miriri.

Vesi 3: *"Ndipo anadza mngelo wina, naima pa guwa la nsembe, nakhala nacho chotengera cha zofukiza cha golidi, ndipo anampatsa zofukiza zambiri, kuti aziike pamodzi ndi mapemphero aoyera mtima onse pa guwa la msembe la golide, lokhala ku mpando wa chifumu."*

Vesi 4: "Ndipo utsi wa zofukiza, pamodzi, ndi mapemphero a oyeramtima unakwera kutuluka m'dzanja la mngelo, pa maso pa Mulungu."

Vesi 5: *"Ndipo mngeloyo anatenga mbale ya zofukiza, naidzaza ndi moto wopala pa guwa la nsembe nauponya pa dziko lapansi, ndipo panakhala mabingu, ndi mau, ndi mphenzi, ndi chivomerezi*."

Vesi 6: *"Ndipo angelo asanu ndi awiri, akukhala nao malipenga anadzikonzera kuti aombe."*

Mavesi amenewa akutanthauza kuti angelo asanu ndi awiri auzimu amenewa amene ali mabingu a ku chivumbulutso, chaputala chakhumi, akonzeka kuomba malipenga. Iyi ndi nyengo yakusintha, kuchokera ku Mulungu kuchita ndi Mkwatibwi wa Amitundu ndi kuchitanso ndi pfuko la Israeli. Izi zikuchitika kumwamba, koma ndi nyengo ya nthawi mu dziko. Mulungu akukonzekera kubweranso kachiwiri, kudzayamba kuchita ndi Israeli. Kodi mukuona kusintha uku? Iyi ndi nyengo ya nthawi pakati pa kutsegulidwa kwa zisindikizo zisanu ndi ziwiri ndi nthawi imene lipenga ngakhale limodzi

lisanalire.Kachisi anali m'mene analiri mu mapembedzedwe a ku Chipangano Chakale, pamene amapereka msembe, koma, apa anali mapemphero a oyeramtima amene amapereka. Mngelo wa pa vesi 5 anatenga chofukiza chodzala ndi moto kuchokera pa guwa ndi kuponya pa dziko. Chimenecho chikutanthauza chiyani? Ndikutseka kwa m'bado ndi kukonzekera, kapena kupanga kukonzeka, kuyamba china chake. Uku kunali kupanga gawo la kumwamba kukonzekera kupmba kwa malipenga. Izi zonse zikuchitika mu kanthawi kochepa.

Malipenga awa asanu ndi awiri ndi ntchito ina ya angelo awa, chimene chikutanthauza kuti iwo aomba kale, ngati mabingu kwa mkwatibwi. Chimene chili ndi chakuti mabingu asanu ndi awiri akuyenera kukhala maliu "asanu ndi awiri amenewo"angelo auzimu kubweretsa zotsatira za zimene zachitika kudutsa mibado isanu ndi iwiri ya mpingo ndi kubwezeretsa chidziwitso cha Mulungu, Mau a Mulungu, ndi mphamvu ya Khristu pa dziko. Chimene chidzakhale ndi Khristu pa dziko, monga m'mene Iye analiri mu bukhu la Machitidwe. Kotero mabingu akatha kuomba, mngelo woyamba adzanyamula lipenga ndi kuomba.

Vesi 7: *"Ndipo woyamba anaomba, ndipo panakhala matalala ndi moto, zosakaniza ndi mwazi, ndipo anazitaya pa dziko lapansi, ndipo limodzi la magawo atatu adzikolidapserera, ndipo limodzi la magawo atatu a mitengo lidapserera, ndipo msipu wonse udapserera."*

Pamene malipenga awa aomba pali chinachake chimene chikuchitika mu gawo la uzimu chimene Yohane anachiona, koma dziko limalandira zotsatira za icho. Tayang'anana zotsatira zomwe Yohane adaziona. Akuti, *"ndipo limodzi la magawo atatu amitengo lidapserera ndipo msipu wonse udapserera."* Ichi ndi chimene chidzachitika pa dziko, koma anthu sadzaona gawo loyamba la lipenga, moto, matalala, ndi mwazi zochokera kumwamba.Yohane anaona izi mu Mzimu. Zotsatira za izo padziko zinali zakuti limodzi la magawo atatu amitengo ndi msipu zidapserera. *Limodzi la magawo atatu* amenewo zikutanthauza kuti ndi gawo la ku M'mawa Chapakati padziko la pansi. Malipenga amenewa ndi chenjezo cha chiweruzo cha Mulungu ku Israeli.

Pa nthawi iyi sabata la 70 la Danieli layamba kale. Aneneri awiri akuima ku Israeli ndipo iwo adzakhala amuna okhala ndi mzimu wa Mose ndi Eliya pa iwo, pamene ntchito zawo zikuwaulura iwo ku Israeli. Malipenga amene anaombedwa mu gawo loyamba la sabata la 70 la Danieli udzakhala uthenga wa Mose ndi Eliya. Gawo loyamba la sabata sichisautso, koma padzakhala nthawi ya chilara ku Israeli chimene sichinakhaleponso kuyambira nthawi ya Eliya. Pakuti adzatseka kumwamba ndipo sipadzakhala mvula yakugwa kuchokera ku mwamba ndi kuzungurira Yerusalemu. Komanso, Mose adzaima ndikusintha nyanja kukhala mwazi –zonsezi mu gawo loyamba la sabata.

Mika 7: 15-16 akuonetsa m'mene Mulungu adzachitira ndi Israeli mu tsiku lotsiriza. Akuti, *"Monga masiku akutuka kwako m'dziko la Aigupto ndidzamuonetsera zodabwitsa. Amitundu adzaona nadzachita manyazi ndi mphamvu yawo yonse, adzagwira pakamwa, m'makutu mwao mudzagontha."*

Ife tazolowera kukhala mudziko lotobola batani kumene zonse ndi za otomatiki moti ndikovuta kuti pfuko la Amitundu kuti limvetse m'mene Mulungu amagwiritsira ntchito chilengedwe nthawi zina, ndipo pamene mafuko awa awona izi, iwo adzadabwa ndipo adzati, "Kodi chikuchitika ndi chiyani pa dziko lapansi?" Pamene Mose adzasandutsa nyanja magazi, mafuko mamenewa adzayamba kuziona mwa sayansi, koma Baibulo likuti iwo adzadabwa.

Mika 7:17 akuti, *"Adzanyambita fumbi ngati njoka, ngati zokwawa za padziko, adzanjenjemera potuluka m'ngaka mwawo adzafika kwa Yehova Mulungu wao ndi mantha, adzaopa chifukwa cha iwe."*

Ngati ife tikufuna tione chimene Mulungu akuchita mu Israeli mu zaka zitatu ndi theka zoyambirira za sabata la 70 la Danieli, ife tikhoza mwakanthawi kochepa kuonanso pobwerera ku Aigupto. Pamene iye anachita nao ndipo iye anawatulutsa iwo ku Aigupto, choncho Iye adzachitanso nawo mu tsiku lotsiriza. Kodi Mose sakanakanthe dziko ndi mitundu yonse ya miriri?

Lipenga loyamba lipangitsa limodzi la magawo atatu a mitengo ndi msipu kupserera. Izi zidzachitika ku gawo la dziko. Padzakhala chilala chachikulu dziko silinaonepo kuyambira nthawi ya Eliya weni weni. Ndi chenjezo cha Mulungu ku Israeli, kunena kuti dzuka ndipo funa Mulungu.

Tsopano, Israeli akudzala ma oranje ochuluka, zipatso, ndi zina zotero. Iwo ali ndi zochuluka kuposa zimene akufuna, ndiye akuzitumiza kunja, koma kudzakhala chilala. Pamene pfuko la Israeli lidzasaina pangano ndi papa ndi kuyendera limodzi ndi wotsutsa khristu, Mulungu adzaonetsera kusagwirizana nazo zimenezo. Mneneri ameneyo, Eliya, adzaima pomwepo mu Israeli ndi kukantha dziko ndi kulankhula Mau a Mulungu, mau achiweruzo, ndi kuti, "Pasankhalenso mvula kufikira ine nditaitana iyo." Kumwamba kudzatsekeka, limodzi la magawo atatu, mkati komanso kuzungulira Kum'mawa Chapakati kudzauma, ndipo mafuko amenewo adzaziona izi. Kudzakhala kouma kwambiri moti masamba amitengo adzauma ndipo msipu wonse udzauma.

Tiyeni tiwerenge mavesi ochepa ku Yoweli, kenako tipite ku Chivumbulutso 11 kukuonetserani kuti izi sizikuchitika nthawi ziwiri, koyamba ku Chivumbulutso 8 ndi kena ku Chivumbulutso 11, ndi chinthu chomwecho mu machaputala onsewa. Izi zimangochitika kamodzi, ndipo aneneri kunenera, ndi zotsatira za kuomba kwa malipenga. Mu mzimu muli mngelo akuomba lipenga.

Yoweli 1: 15-17 akuti, "*Kalanga ine, tsikuli! Pakuti layandikira tsiku la Yehova, lidzafika ngati chionongeko chochokera kwa Wamphamvuyonse. Chakudya sichichotsedwa kodi pamaso pathu? Chimwemwe ndi chikondwerero pa nyumba ya Mulungu wathu? Mbeu zaola pansi pa zibuluma zao, zosungiramo zaonongeka, nkhokwe zapasuka, pakuti tirigu wakwinyata.*" [Chifukwa sikunagwe mvula m'monga mwa kunenera kwa Eliya.]

Aneneri awiri akuyesera kuchenjeza pfuko la Israeli ndipo padakali chifundo pokhapokha aneneri awiri akuima kumeneko, koma Ayuda andale awo adzapanga pangano ndi wotsutsakhristu, ndipo Mulungu samazikonda izo. Iye "adzadula madzi" ndipo sikudzagwa dontho, kukwaniritsa Mau a Mulungu.

Apa pali chimene chimachitika m'munda: mbewu idzaora m'munda ndipo zosungiramo zidzaonongeka. Izo sizinaonongeke pano zikuphulika chifukwa zadzaza. Israeli akuyesera kutumiza kunja zochuluka ndi zochuluka kugulitsa ku maiko ena. Chifukwa chiyani? Dziko likubeleka, chipululu chikuphukira, ndipo sangathe kuchita chili chonse ndi zimenezi akupeza. Mulungu akusekerera Israeli lero, koma yang'anani pamene lipenga ili lidzaomba. Minda yonse idzauma ndipo tirigu adzakwinyata.

Yoweli 1:18 akuti, "*Ha! Nyama ziusa moyo, magulu ang'ombe azimidwa; pakuti zisowa podyera; magulu ankhosa omwe atha.*" Chifukwa chiyani izi? Mngelo waomba lipenga ndipo Eliya wanena, "Pasakhalenso mvula" ndipo chilichonse mu Israeli chikuuma. Ngakhale ng'ombe zilibe msipu wobiriwira.Yoweli 1:19- "*Ndipfuulira kwa Inu Yehova, pakuti moto wapsereza mabusa a m'chipululu, ndi malawi a moto anatentha mitengo yonse ya kuthengo.*" Izi zikunena kuti moto waononga nsipu wa mu chipululu. Izi sizikutanthauza kuti wina anaponya matcheso ndipo anaotcha msipu onse. Ndi chilala, chilala chachikulu chomwe dziko silinachidziwepo kuyambira nthawi ya Eliya.

Pamene akunena kuti gawo limodzi la magawo atatu amitengo ndi msipu wobiriwira lapserera, zikutanthauza kuti pali nthawi yaikulu ya chilala, zaka zitatu ndi theka, ndipo msipu wapserera.Yoweli akuzitchula kuti moto kuyatsa minda ndi malawi a chilala chachikulu. Sipadzakhala mvula ndipo msipu udzakwinyata. Ndi chiweruzo cha Mulungu nthawi imeneyo.

Yoweli 1:20 akuti, "*Inde nyama zakuthengo zilira kwa inu, pakuti mitsinje ya madzi yaphwa, ndi moto wapsereza mabusa a m'chipululu.*" Mu masiku a Eliya, kodi kakhwawa sikanaphwe kumene Eliya amakhala? Kunali njala mu tsiku limenelo ndipo madzi anali osowa. Idzakhala nthawi yovuta, koma pakadali chisomo; chifukwa pali aneneri awiri apa. Mulungu nthawi zonse amatumiza chenjezo asanatumize chiweruzo. Ichi sichiweruzo chopanda chifundo, ichi ndi chenjezo cha chiweruzo. Mu bukhu la Mika Iye anati adzachita ndi iwo monga anachitira pamene iye amawatulutsa kuchokera ku Aigupto.

Tiyeni tiwerenge mu chaputala cha khumi ndi chimodzi cha Chivumbulutso kukuonetserani inu kuti ichi ndi chinthu chomwecho. Zikuchitika ndi ichi mu gawo la lalikulu mu kufotokoza

Chivumbulutso 11:3 akuti, "*Ndipo ndidzalamulira mboni zanga ziwiri, ndipo zidzanenera masiku chikwi chimodzi ndi mazana awiri mphambu makumi asanu ndi limodzi, zovala chiguduli.*" Izi ndi kwenikweni zaka zitatu ndi theka.

Tayang'anani chinanso chimene akuchita. Chivumbulutso 11:6 akuti, *"Izo zili nawo ulamuliro wakutseka mwamba, isagwe mvula masiku a chinenero chao, ndipo ulamuliro zili nao pa madzi kuwasandutsa mwazi, ndi kupanda dziko ndi mliri uli wonse nthawi ili yonse zikafuna."* Izi ndi zaka zitatu ndi theka za chilala zimene takhala tikuwerenga za izo. Uwu udzakhala mzimu wa Eliya kubweranso mwa munthu wina ndipo iye adzati, "Pasakhalenso mvula mpaka ine nditaitana iyo." Ndipo sipadzakhalanso mvula, msipu udzakwinyata, ndipo mbewu zidzavunda pansi pa nkhaka, ndi zina zotero. Padzakhala chilala chachikulu mu dziko la Israeli. Gawo limodzi la magawo atatu amitengo ndi msipu zidzapserera.

Ndi ndani amene anasandutsa madzi magazi mu masiku a Baibulo? Mose. Iye anasandutsa madzi kukhala magazi mu dziko la Aigupto. Kodi aneneri awiri awa adzakhala ndani? Mose ndi Eliya.

Lotsatira la vesi ili likuti, *"Ndi kupanda dziko ndi mlili uli wonse nthawi iliyonse zikafuna."* Iwo sakungotseka kumwamba, iwo sakungosandutsa madzi mwazi, koma akukantha dziko mochuluka m'mene angafunire.

Kodi Mose anachita chiyani ku Aigupto? Iye sanangosandutsa madzi kukhala magazi koma iye anaitana msabwe ndipo msabwe zinabwera. Iye anaitananso m'dima ndipo panali m'dima pa dziko kwa masiku atatu. Pamene Mulungu anachita ndi Israeli pamene iye amawatulutsa mu Aigupto chomwecho adzachita nawo mu tsiku lotsiriza.

Taonani, awa ndi angelo womwewo asanu ndi awiri, ndipo iwo akuomba malipenga tsopano. Uku ndi kuitana chiweruzo, kuchenjeza Israeli ndi kuti; "Iwe wamvera chirombo, ndipo tsopano uchenjere, khala mu nzere ndipo mvera aneneri." Uwu ndi utumiki wa aneneri awiri.

Mu gawo la kumwamba apa, mngelo akuomba lipenga, koma mu gawo lapansi angelo awiri akuima apa akunenera. Kodi inu mukuona lipenga loyamba? Lipenga loyamba ndi chilala. Ndi uthenga wa Eliya, mneneri kutseka ku mwamba kuti kusagwe mvula. Limenelo ndi lipenga loyamba. Tiyeni tiombe lipenga la chiwiri.

Vesi 8: *"Ndipo mngelo wachiwiri anaomba, ndipo monga ngati phiri lalikulu lakupserera, ndi moto linaponyedwa m'nyanja; ndipo limodzi la magawo atatu anyanja linasanduka mwazi."*

Vesi 9: *"Ndipo lidafa limodzi la magawo atatu azolengedwa zili m'nyanja, zokhala ndi moyo, ndipo limodzi la magawo atatu azombo lidaonongeka."*

Nyanja ya Mediterrane, ndi madzi ozungulira Israeli adzakhala chikoka cha dziko la pansi. Zidzakhala pa mitu ya nkhani, pa mawailesi akanema ndi zina zotero. "China chake chikuchitika ku Israeli, nyanja yasanduka magazi."

Anthu aku Israeli sadzayang'na ndi kuona phiri lalikulu likugwera mu nyanja, koma iwo adzaona munthu, Mose, ataima pamenepo ndi kunena kuti, "Ngati inu simukukhulupirira kuti ndine mneneri wa Mulungu amene ndadzuka, ndiye nyanja isanduka magazi." Iye adzalankhula Mau ndi kusandutsa nyanja yonse ya Mediterrane magazi, imeneyo kukhala limodzi la magawo atatu anyanja. Inu musaike maso anu pa Pacific, Atlantic, kapena nyanja ya India. Zidzachitika mu nyanja ya Mediterrane.

Mafuko onse ozungulira nyanja ya Mediterrane asanaone Israeli, iwo akuyenera kuyang'ana nyanja. Baibulo likuti iwo adzakwawa kutuluka m'mayenje ngati mbozi. Iwo adzati, "Kodi chikuchitika mu dziko ndi chiyani?" Ndi aneneri awiri amene Mulungu ali nao mu Israeli; ndi chimene chikuchitika. Ndi Mulungu kuyendera Israeli kubweretsa Mau ku kukwaniritsidwanso mu tsiku lotsiriza.

Pamene 144,000 adzaona kuti nyanja yasandulika magazi, ndi kuona palibe mvula imene ikubwera, iwo adzawakhulupirira aneneri awiri. Padzakhala 144,000 osindikizidwa kupita kukalalikira Uthenga Osatha wa chaputala chakhumi ndi chinai cha Chivumbulutso. Sipadzakhala phiri la moto kugwera mu nyanja pamene mngelo uyu aomba. **Iyi ndi njira chabe ya Mulungu yobisira Mau mpakana Iye atakonzeka kuulura iwo.**

Lipenga loyamba ndi chilala pa dziko la Israeli monga Eliya mneneri, analankhula Mau. Lipenga lachiwiri ndi Mose kusandutsa nyanja kukhala magazi. Tiyeni tipite ku lipenga lachitatu.

Vesi 10: "*Ndipo anaomba mngelo wachitatu, ndipo idagwa kuchokera kumwamba nyenyezi yaikulu, yoyaka ngati muuni, ndipo idagwa pa limodzi la magawo atatu a mitsinje, ndi pa akasupe a madzi."*

Vesi 11: "*Ndipo dzina lake la nyenyeziyo alitcha Chowawa; ndipo limodzi la magawo atatu a madzi lidasanduka chowawa; ndipo anthu ambiri adafa pakumwa madzi; pakuti anasanduka owawa."*

Chinachake chidzachitika, ndipo Mulungu adzachita chinachake kusokoneza mitsinje ndi timitsinje mu Israeli ndi kuzungulira maiko a Kum'mawa Chapakati, adzasanduka owawa oti munthu sangamwe.

Anthu sadzaona nyenyezi ikugwa, koma adzayang'ana pa madzi. Madzi adzasintha mtundu ndikuyamba kuwawa mpakana sadzatha kumwa iwo. Chidzakhala chiyani? Adzakhala aneneri awiri kukantha madzi. Iwo adzalankhula mau a chiweruzo ndi kuti, "Mtsinje uliwonse mu Israeli ukhale owawa kuti anthu asamwe madzi, chifukwa mwakana Mau a Mulungu." Izi zikuchitika mwa mau a aneneri. Mugawo la uzimu angelo akubwera ndi kuomba lipenga.

Tsopano, kodi Mose anachita chiyani mu dziko la Aigupto? Mose anaitana m'dima mu dziko la Aigupto ndipo kunali m'dima wambiri mwakuti zinakhala ngati kuti amatha kukhudza m'dima. Taonani pamene lipenga lachinai ili liomba.

Vesi 12: "*Ndipo mngelo wachinai anaomba, ndipo limodzi la magawo atatu a dzuwa linagwidwa, ndi limodzi la magawo atatu a mwezi, ndi limodzi la magawo atatu a nyenyezi; kuti limodzi la magawo awo atatu lidetsedwe, ndi kuti limodzi la magawo ache atatu a usana lisawale, ndi usiku momwemo."*

Chifukwa chiyani zinali limodzi la magawo atatu aizi basi? Chifukwa likukhudza mkati komanso kuzungulira maiko a Kum'mawa Chapakati amene azungulira Israeli, monganso ku Aigupto. Mulungu anati, monga anachitira nawo pamene amawatulutsa mu Aigupto, chomwechonso adzachita nao mu tsiku lotsiriza. Munali m'dima mu dziko la Aigupto, ndipo kudzakhalanso m'dima mu Israeli. Tsopano monga mudzaona, palibe chotsala koma chiweruzo. Izi zikutifikitsa ife ku pafupifupi pakati pa sabata la 70 la Danieli.

Pamene mngelo wachinai uyu aomba, Mulungu adzazimitsa kuwala mwa kanthawi pang'ono, kuonetsa Israeli kuti kukufuna kude ndipo pakubwera nthawi imene ziwanda zidzatuluka. **Ichi ndi chenjezo chotsiriza cha Mulungu kwa Israeli.**

Malipenga anai oyamba awa ndi chenjezo la kwa Israeli kuti avomere njira ya Mulungu ndi kukana wotsutsakhristu. Panthawi iyi, zaka zitatu ndi theka zadutsa, ndipo ndi pafupifupi pakati pa sabata. Kenako mngelo akubwera kuuluka kudutsa mwamba kulengeza miriri itatu imene idzachitike pamene lipenga lachisanu liomba.

Vesi 13: "*Ndipo ndinaona, ndipo ndinamva chiombankhanga chirikuuluka pakati pa mwamba, ndikunena ndi mau akulu, Tsoka, tsoka, tsoka, iwo akukhala pa dziko, chifukwa cha* ***mau otsala*** *a lipenga la angelo atatu asanaomb!"* [Awa ndi angelo omwewo amene adalankhula mu chaputala cha khumi, vesi la chinai la Chivumbulutso.]

Tsopano, pali miriri itatu apa, ndi pakati pa sabata. Ine ndikufuna ndikuonetsereni inu chimene miriri iyi ili.

Tsoka loyamba lalembedwa mu Chivumbulutso 9:1-12. Dzenje la phompho latsegulidwa ndipo ziwanda zonse zatuluka kudzazunza anthu, ndipo iwo adzati kudzakhala bwino kufa.

Tsoka lachiwiri lalembedwa mu Chivumbulutso 11:7-14, ndipo ndi wotsutsakhristu kupha aneneri awiri a Mulungu. Izi zikuimitsa chifundo cha Mulungu ndi liu la Mulungu. Palibenso chifundo cha mtundu uwu. Palibe chilichonse koma chisautso chachikulu. Iyi ndi nthawi ya mavuto aYakobo pamene kudzakhala chisautso chachikulu.

Tsoka lachitatu lili pa Chivumbulutso 12:7-17. Chirombo chaponyedwa kuchoka ku gawo la kumwamba, kutanthauza kuti mphamvu zonse za satana, mdierekezi mwiniyekha, wabwera ndipo wakhala mwa papa. Iye akusautsa Israeli, mai wa pa Chivumbulutso chaputala 12, ndipo iye akupha oyeramtima aku chisautso awo. Satana mwiniyekha adzamasulidwira thupi la munthu. Iye adzapitirira ndi kupha mbewu ya mzimai ndi iwo amene amasunga malamulo a Mulungu ndi kukhala ndi umboni wa Yesu.

Kodi mukuwaona matsokawa? Mngelo kuuluka kudutsa ndi kumanena kuti chifundo chatha ndi kuti, *"Tsoka, tsoka, tsoka, kwa okhala pa dziko."* Kulengeza kwa matsoka atatu amenewa kukupangika pakati pa lipenga lachinai ndi lachisanu, ngakhale, matsokawa sakuchitika mpakana lipenga lachisanu liombe. **Matsoka atatu onsewa amasulidwa mwa kuomba kwa lipenga lachisanu ndipo zotsatira za iwo zikupitirira pansi pa lipenga la chisanu chimodzi komanso lipenga lachisanu ndi chiwiri.** Pamene lachisanu ndi chimodzi ndi lachisanu chiwiri liomba mu gawo lotsiriza la sabata, kuchuluka kwa chikhalidwe ichi chimene matsoka atatu anayambitsa chidzaipira ndi kuipirabe. Ndi chifukwa chake malipenga atatu otsiriza akutchulidwa pa kulengeza kwa matsoka atatu. Kachiwirinso, matsoka onse atatu ikuchitika pansi pa lipenga la chisanu, ndipo ndi penipeni pakati pa sabata la 70 la Danieli.

Potsiriza, *lipenga loyamba* ndi Eliya kutseka kumwamba kuti isagwe mvula. *Lipenga lachiwiri* ndi Mose kusandutsa madzi magazi. *Lipenga lachitatu* ndi madzi mutsinje kusanduka owawa, anthu kumafa akawamwa. *Lipenga la chinai* ndi Mulungu kuzimitsa kuwala ku gawo limodzi la magawo atatu a tsiku. Zonsezi zikuchitika ku Israeli. Kenako mngelo wachisanu asanaombe, mngelo akuuluka kudutsa mwamba ndi kulengaza matsoka atatu amene adzachitika pamene mngelo wachisanu aomba lipenga lake pakati pa sabata.

Chaputala ichi chachisanu ndi chitatu ndi uthenga wa aneneri awiri ndi anai a angelo kuomba malipenga awo. Gawo loyamba la chaputala ichi ndi kanyengo kosintha pang'ono Mkwatibwi atatha kukonzekera Mkwatulo, ndipo lipenga lisanaombe ku Israeli monga vesi lachitatu kudutsa lachisanu ndi chimodzi akuonetsera. Amen.